


# CHISINDIKIZO CHA MULUNGU

 . . . -tsitsimutso, basi cha mtundu wa kachitidwe- kachikale chimene ife tinkakhala nacho zaka zambiri zapitazo, ndipo ife tiri oyamikira kwambiri chifukwa cha ichi. Ndipo ine ndikuyamikira kuyimba kowonjezera uku, kuyimba konse, ndi zapadera izi. “Ine ndapita mtunda wotsiriza wa njira; kupuma pa kutsekera kwa tsiku.” Ndi pamene, mwinamwake, kungokhala pano, pamene iwo anali kuyimba iyo, kuyang’ana kunja ndi kumawona dzuwa pamene ilo likulowa; mbalame zonse zikuyimba motsika ndi mofewa, zonse ziri pafupi kuchoka tsopano ndipo izo zapita kukapuma, mawa mmawa kuti likatuluke kwa tsiku latsopano.

<sup>2</sup> Ndipo umo ndi momwe izo ziriri ndi moyo; masiku ogwirira ntchito posachedwapa akupita, ndipo ife tidzagona pa kama wathu. Ine ndidzakonda kuyankhula kwa Iye tsiku limenelo, basi kuyankhula kwa Iye. Kusonkhanitsa zovala zanga pozungulira ine, ndi kulowa mu chipinda.

<sup>3</sup> Podziwa ichi, monga Paulo Woyera ananena kalelo, “Ine ndikumudziwa Iye mu Mphamvu ya chiwukitsiro Chake.” Kuti, pamene Iye adzayitana ndituluke kuchokera kwa akufa, ine ndidzayitanidwa ndituluke nawo iwo.” Kumudziwa Iye mu Mphamvu ya chiwukitsiro Chake.” Osati kumudziwa Iye mwa mawu kapena mwa ntchito, koma kumudziwa Iye mu Mphamvu ya chiwukitsiro Chake. Ndicho chimodzi cha zathu—ziyembekezera zathu zazikulu usikuuno, ndipo chiyembekezo chokha chimene ife tiri nacho, chiri mu . . . chiwukitsiro chachikulu chija cha Ambuye wathu Yesu; ndipo chiwukitsiro chathu choyambirira chimene ife tiri nacho tsopano, kuchoka kwa akufa kupita ku Moyo, mwa kukhala nawo Moyo Wamuyaya kupyolera mwa Yesu Khristu.

<sup>4</sup> Kuyembekezera, ndi kuyembekezera kwaulemerero, kwa chirengedwe chonse, mpaka tsiku limenelo pamene Iye ati adzabwere nthawi yachiwiri, kuchokera Kumwamba, Amene Mulungu ati adzamutumize mu nthawi yake. Ndiyeno matupi achivundi awa, amene ife tikubuuliramo tsopano, adzatenga chisavundi, “Ndipo ife tidzasinthidwa ndi kupangidwa ngati thupi Lake Lomwe laulemerero, pakuti ife tidzamuwona Iye monga Iye aliri.”

Ndiye tchimo ndi chisoni, tchimo ndi imfa za dziko la mdima ili zidzatha,

Mu ulamuliro waulemerero uwu ndi Yesu wa zaka chikwi za mtendere.

<sup>5</sup> Mbalame zikuyembekezera chimenecho. Mitengo ikuyembekezera chimenecho. Chirengedwe chonse chikupindika

ndi kulirira, kuyembekezera nthawi imeneyo, kubuulira kuti chivekedwe pa icho.

<sup>6</sup> Msungwana wanga wamng'ono, kanthawi kapitako, anandifunsa ine funso. Iye anati, "Adadi, kodi dziko lapansi ili linkawoneka ngati chiyani pamene Mulungu anathana nalo ilo?"

<sup>7</sup> Ine ndinati, "Ilo linali lokongola, wokonedwa. Ilo linali lokongola." Ndipo ine ndinati, "Tsiku lina lidzakhala ngati choncho kachiwiri, pamene themberero liti lidzachotsedwepo. Ndiyeno ife tidza. . . Ilo lidzakhala monga ilo linali pachiyambi, paradiso wamkulu wa Mulungu."

<sup>8</sup> Tsopano, molunjika kupita mu ntchito. Ine ndinali kuganiza tsopano, usiku woyamba. . . Uno ndi usiku wachitatu wa chitsitsimutso chatu chaching'ono. Ndipo ife sitinakhale nawo msonkhano wamachiritso. Ndi kutakasuka chabe, basi kuti tifotokozere kumverera kwathu, ndi kuphunzitsa Uthenga mwa njira ya kachitidwe-kachikale; Uthenga womwewo umene ine ndinkaphunzitsa kuno, zaka zambiri, mbiri zapitazo, sindinasinthe kachidutswa kamodzi. Ndiko kulondola, Uthenga womwewo basi, popanda kachidutswa kowupanga mwatsopano kapena kuwupukuta; basi Uthenga womwewo.

<sup>9</sup> Kunja mu misonkhano, pokhala azipembedzo zosakanikirana, pa maziko a kukhala mu nyumba yolankhuliramo ndi zipembedzo zambiri zosiyana za anthu atabwera pamodzi, iwe umakhala ngati umadzigwira wekha kwa Chiphunzitso; zonse kupatula machiritso Auzimu, ndi, ndithudi, kulandira kwa Ambuye Yesu. Koma pamene iwe uli kwanu, ngati mpingo wakwathu kuno, iwe umangomverera ngati kuti ungochotsa kolala yako, ndipo basi mophweka kumangolalikira chimene iwe ukuganiza kuti chiri cholondola, ndipo ndi chimenecho.

<sup>10</sup> Ndipo nthawi zambiri, mkati muno, tiri nazo, nthawi zambiri, anthu samagwirizana nazo. Ife sitingakhoze kuyembekezera aliyense kuti azigwirizana nafe ife pa Chiphunzitso chatu cha mpingo ndi zinthu zimene ife tiri nazo. Koma tikanati mwinamwake ife tikanakhala chinthu chomwecho, ngati abusa anu akanakhala akulalikira, koma iwo akanakhalabe m'bale wanga. Musakhale, osalabadira izo. Ndipo aliyense amayang'ana pa zinthu mwa kupenya kosiyana.

<sup>11</sup> Ndipo mu sabata lino, powona kuti ine ndimayenera kulepheretsa sabata mu Canada, pa chifukwa cha mkuntho wa chisanu, bwanji, izo zinandipatsa ine mwayi woti ndifike pobwera kuno ku kachisi ku chitsitsimutso cha mausiku angapo, chimene ine ndinalonjeza pamene ine ndimachoka. Ndipo ine ndikupereka izo, kuti uko kunalibe. . . "popanda msonkhano wa machiritso; kulalikira Uthenga kokha." Basi. . . Ndipo pa uwu, kupeza, ine ndimaganiza mwinamwake ife tikanatenga mausiku angapo pa Mibadwo Isanu ndi iwiri ya Mpingo. Pakuti ine

ndikukhulupirira moona kuti ife tikukhala mu m'badwo wa mpingo wotsiriza, tsiku lotsiriza, basi kusanafike Kudza kwa Ambuye Yesu.

<sup>12</sup> Ine nthawizonse ndimayesera kudziyeza ndekha, mpingo waung'onowu pano, kulikonse kumene ine ndakhala ndikuyankhula, chifukwa chakuti Ambuye wabwino Wakumwamba wandipatsa ine pang'ono pokha pa utumiki, uwonso, wa ku mbali ya zauzimu, monga inu mukumvetsera. Ndipo anthu amakangamira ku mawu ako, ndipo—ndipo kotero ine—ine ndiyenera kukhala wosamala kwambiri zimene ine ndiri kuyankhula. Chifukwa, ngati Mzimu Woyera wapereka mphanvu iyi ya masomphenya ndi kuzindikira za mu mtima, zimene ziri zosatsutsika, ndipo iwo amakumva iwe ukuyankhula, iwo amamverera kuti iwe uli nalo lingaliro lina la zimene iwe ukuziyankhula, kapena Mulungu sakanati azidalitsa konse cholakwika ndi kuchitumiza icho kunja monga choncho. Mwaona? Kotero ndiye iwe uyenera kukhala osamalitsa kwambiri, ndi kuchiyeza icho mu kuwala kwa Mawu, nthawi zonse. Ndipo mmenemo, ngati ine ndilakwitsa, ine ndimapemphera Mulungu kuti andikhulukire ine, chifukwa ine sindimatanthauza kutero. Ndipo ine . . .

<sup>13</sup> Ndipo nthawi iliyonse, mu kuphunzitsa, ndipo makamaka mu maphunziro akuya awa amene ife tirimo tsopano, ndi usiku watha pa *Chilemba Cha Chirombo*, ndi maphunziro monga amenewo, ndipo usikuuno wa *Chisindikizo Cha Mulungu*, chilemba cha Mulungu, ndi zina zotero monga choncho, ine ndikumverera kuti mwinamwake, ine ndikhoza kukhala nawo ochuluka amene sangagwirizane ndi izi, ndi zimene ine ndimaphunzitsa pa izo. Koma ine ndimayesa kuchita izo basi ngati. . . osati kulondolera Izo kwa mpingo uliwonse, chipembedzo chirichonse, kapena anthu aliwonse, osati konse. Mulungu amadziwa zimenezo. Basi mu Kuwala kumene ine ndimawonera izo mmenemo, ndimo momwe ine ndimayankhulira izo.

<sup>14</sup> Ndipo palibe mpingo umene umadzitcha Dzina la Ambuye Yesu koma umene ine ndimawukonda. Mwakuti palibe munthu amene angakhoze kutcha Dzina Lake, kapena kukhala nako kulemekeza kulikonse kwa Iye, koma chimene ine ndingakhoze kupita ku imfa yanga kuti ndiwachitire iwo chirichonse. Ndiko kulondola. Ziribe kanthu kaya ndi chizindikiro chanji chachipembedzo chimene iwo akuvala, kaya ndi Amethodisti, Abaptisti, Akatolika, chirichonse chimene chingakhale, izo sizingakhale vuto laling'ono kwa ine. Ndiko kulondola. Malingana ngati iwo ali nako kulemekeza kwa Ambuye wanga.

<sup>15</sup> Koma, tsopano, pali Choyang'anapo. Ndipo tsopano mpingo uliwonse umaphunzitsa, mwinamwake, chimene zamulungu zawo ziri za mpingo umenewo, pokhulupirira kuti zakhazikitsidwa pa Choyang'anapo. Chabwino, tsopano, nthawi

zambiri, mu kupenya zinthu zimenezo, kuti izo siziri momwe ine ndimawerengera Choyang'anapo, kotero ndiye ine ndiri nawo ufulu mu mpingo wanga womwe kuyala chimene ine ndikuganiza kuti chiri cholondola.

<sup>16</sup> Kuno nthawi yina kalepo, womanga... Ine ndinali mu Milltown, ku Milltown Baptist church, kumene ife tinali ndi chitsitsimutso. Ndipo M'bale Wright ndi inu nonse, ine ndikuganiza, mukumukumbukira Marion Lee. [M'bale George Wright akuti, "Ameni."—Mkonzi.] Ndipo iye anali wokwiya kwambiri pa chinachake chimene ine ndinaphunzitsa pa ubatizo wa madzi. Chabwino, iye anapita kwawo, ndipo iye anali wokwiya pa izo. Ndipo iye anali womanga.

<sup>17</sup> Usiku umenewo iye analota loto. Ambuye anamusonyeza iye kuti iye anali kumanga nyumba, ndipo iye anali woti ayike zenera lotulukira pa iyo. Ndipo kotero mmalo moyika zenera lotulukira pa iyo, iye anangoika khonde, anati, "Izo zikhala bwino." Kotero pamene mwiniwake wa nyumba anabwera uko, anati, "Igwetsere iyo pansi mpaka ku maziko; iyambenso mobwereza kachiwiri."

<sup>18</sup> Kotero iye anali ataphunzitsidwa chinachake chosiyana ku chimene Baibulo limaphunzitsa, kotero iye anati, "Ine kulibwino ndingogwetsera pansi mazikowa ndi kuyimanganso iyo mobwereza kachiwiri." Ine ndinapita kunyumba ndi iye usiku umenewo, tinakakhala usiku wonse ku nyumba yake. Kotero ndiye ife. . .

<sup>19</sup> Izo ndi zoono. Izo ziyenera kuti zikhale zoyalidwa. Ndipo, pophunzitsa maphunziro awa, ine sindine mphunzitsi. Koma mu zimene ine ndikudziwa za Iwo, ine ndimakonda kuwafotokoza Iwo kwa ena, ndi kuchita chiyanjano pozungulira Mawu, pamene Mzimu Woyera ukuwapanga iwo enieni kwa mtima wathu. Ndipo kotero ife tikungokhala nayo nthawi yaikulu pochita izi.

<sup>20</sup> Ndipo kungokhala ngati kumupumitsa m'busa wathu wokonedwa pano, M'bale Neville. Ngati pali alendo mu zipata zathu, mwamuna, *apa*, ndi m'busa wathu, M'bale Neville, mwamuna wa Mulungu, wantchito woona wa Ambuye Yesu Khristu. Ine sindikunena izo chifukwa chakuti iye wakhala pano. Ine ndimanena izo kumbuyo kwake komwe, kapena kulikonse, iye wakhala mwa njira imeneyo chimudziwireni ine iye. Iye anali mosamalitsa wa Methodisti, ndipo ine ndinali mosamalitsa wa Baptisti, koma ife tinali abale limodzi, ndipo kotero ife tonse tinatembenuka kukhala oyera-odzigidubuza. Chabwino, sichoncho, m'bale? Ameni. [M'bale Neville akuti, "Ameni. Aleluya!"—Mkonzi.] Kotero ife tikuyima mu bwalo lachiyanjano.

<sup>21</sup> Chabwino, ife, ife tikukhala nayo nthawi yodabwitsa mwa njira iyi, "Kungokhala nacho chiyanjano wina ndi

mzake, pamene Magazi a Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu, akutiyeretsa ife ku kusalungama konse.” Kotero ife tikukhala nayo nthawi yaikulu, ndipo ife ndithudi tikuyamikira alendo mu zipata zathu, usikuuno, pano.

<sup>22</sup> Chitsitsimutso chathu chaching’ono, ine ndikuganiza inu mukudabwa chifukwa chimene icho sichinalengezedwe. Chabwino, iyo inali chabe nthawi yaing’ono ya chisangalalo kwa mpingo wathu kuno, ndipo ndicho chifukwa ife kapena mwinamwake... Ine sindikudziwa momwe Mzimu Woyera uti utitsogolere, koma mwinamwake usiku umodzi, ife tisanatseke pano, ife mwinamwake tingakhale ndi msonkhano wamachiritso, ngati Ambuye alola. Ndipo kotero ine ndikudalira kuti Iye apereka izo.

<sup>23</sup> Ine ndiyenera kubwerera ku Canada tsopano, kukapitiriza mu zitsitsimutso. Ndipo monga nonse mukudziwa, ife tiri ndi dongosolo lolemera ndithu, lodzaza mpaka ku deti ya nthawi yodzapita kutsidya kwa nyanja. Ndipo madongosolo apangidwa kale, kuyambira mu Durban, South...mu Johannesburg. South Africa, mu Septembala, pafupi la chitatu. Ndiyeno ife tikupitirira kuchokera kumeneko kupita ku Durban; ndi ku India; ndi ku Palestina; ndi Luxemburg; ndi Frankfurt; ndi Transjordan; ndi konse kupyola kumeneko. Kubwerera mmbuyo kumudzi pamene Ambuye atsogolera kubwerera, pamene Iye atiuza ife kuti tibwerere. Ndiye iwo akukonza ulendo wina wa ku New Zealand ndi Australia, ndi mpaka kupyola kumeneko; ndipo mpaka kummawa, ku Japan, ndi maiko amenewo kumeneko.

<sup>24</sup> Ine ndikumverera kuti mipingo yambiri kuzungulira kuno, kumene anthu, o, mai, akungokhala ngati akuberana, wina ndi mzake, ndipo, ndiye, zikwi za anthu sizinayambe zamva konse ngakhale za Yesu nthawi yoyamba. Ndipo kotero ine ndikumverera kuti...Ndiko kumverera kwanga, mwandekha, ndi ntchito yanga kuti nditengere Uthenga kwa iwo, mwakupambana kumene ine ndingakhoze. Ndipo tsopano pamene ine... .

<sup>25</sup> Ndiroleni ine ndinene kachiwiri tsopano, chifukwa, akhala pano, Amethodisti, Abaptisti, Akatolika, Apresbateria, Apentekoste, Apilgrim Holiness, Anazerini, akhala pano, ndipo ndicho chimene ife tapangidwira... Ine ndikukhulupirira ndimo momwe ziti zikakhalire Kumwamba, kukhala ngati, gulu lonse la ife titakhala kumeneko.

<sup>26</sup> Ndipo tsopano pa mauthenga awa, monga *Chilemba Cha Chirombo*, ndipo lero pamene pali chisokonezo choterechi... Kodi inu munazimvetsa izo, usiku watha? Ngati inu munatero, nenani, “Ameni.” [Osonkhana anena, “Ameni.”—Mkonzi.] Tsopano ife tati tiyankhule usikuuno pa chilemba cha

Mulungu, kapena, *Chisindikizo Cha Mulungu*. Tsopano ife tikuzindikira . . .

<sup>27</sup> Tsopano, ine sindikungoyesera kuti ndilalikire kuchokera mu ma Baibulo awiri; limodzi ndi lokwanira. Koma ine ndiri nalo limodzi la iwo pano kwa cholinga cha zolembedwa zapansi, ndi zina zotero, za kulozerapo, ngati winawake atati afunse funso. Ndipo tsopano, mawa usiku, ngati Ambuye alola, nditatha kulalikira . . .

<sup>28</sup> Usiku woyamba, pa *Mibadwo Isanu ndi iwiri ya Mpingo* kuwona pamene ife tinali, ife tiri, mwapamalo, mu tsiku limene ife tikukhalamo.

<sup>29</sup> Usiku watha, pa chigawenga chachikulu kwambiri chimene chiripo mu dziko, *Chilemba Cha Chirombo*.

<sup>30</sup> Ndipo, usikuuno, pa dalitso lalikulu kwambiri lomwe liripo mu dziko, *Chisindikizo Cha Mulungu*.

<sup>31</sup> Mawa usiku, ine ndikupatsani inu mwayi kuti muwombere pa ine, tsopano. Mawa usiku ndi mafunso, ndi zinthu zimene inu simukuzimvetsa zokhudza zimene zakhala zikulalikidwa. Inu mwakhala njonda ndi dona mokwanira, kapena Mkristu mokwanira, ine ndingatero, posunga mtendere wanu mu nthawi ya misonkhano. Ine ndikufuna inu muwalembe, mawa usiku pamene inu mukubwera ku mpingo, ndipo mubwere molawirira basi monga inu mungathere, chifukwa ine ndidzayenera kubwera molawirira kudzawerenga ndi kukhala ngati kuwayankhanso iwo, za chimene funso lanu liri lokhudza Lemba.

Ndiye Lamlungu mmawa ndi Sande sukulu yozolowereka.

<sup>32</sup> Lamlungu usiku, mwinamwake Lamlungu usiku, ndi msonkhano waubatizo. Pali anthu ena oti abatizidwe. Ndiyene Lamlungu usiku, ife tidzatero mwinamwake, mwina kukhala ndi Uthenga wolalikira kapena msonkhano wamachiritso. Ife tidzawona chirichonse chimene Ambuye ati adzatitso golere kwa usiku umenewo, kwa Lamlungu usiku, uthenga pa zimenezo.

<sup>33</sup> Tsopano ife tikupeza, ife tisanati tiyandikire izi, kuti, “Palibe munthu Kumwamba, panalibe munthu pa dziko lapansi, kapena panalibe munthu panso pa dziko lapansi, anali woyenera kuti atenge Bukhu, kapena kuti alitsegule Ilo, kapena kumatula Zisindikizo zakezo.” “Panalibe munthu!” Yohane anawona izo mu Chivumbulutso. Ndipo ife tikuphuzitsa Chivumbulutso tsopano. “Ndipo Yohane analira. Koma uko kunali Mwanawankhosa amene anali ataphedwa, kuchokera ku maziko a dziko; Iye anali woyenera kuti abwere ndi kulitenga Bukhu kuchokera mu dzanja lamanja la Iye amene anakhala pa Mpandowachifumu, ndi kuti alitsegule Bukhu, ndi kuti amatule Zisindikizo zakezo.” Ndipo Mwanawankhosa ameneyo, ndithudi, anali Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu. Ndipo tsopano ngati Iye ali Mmodzi yekha yemwe ali woyenera . . .

<sup>34</sup> Iye anakhalapo kuno kamodzi ndi ife, pa dziko lapansi, mu mawonekedwe a Munthu. Mulungu ankakhala mwa Mwana Wake, Khristu Yesu, ngati Mulungu-Munthu.

<sup>35</sup> Ndipo Iye anabwerera kupita mu Ulemerero, kusiya Mawu awa, “Kanthawi pang’ono ndipo dziko silidzandiwonanso Ine. Komabe, inu mudzandiwona Ine, pakuti Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, mpaka ku mapeto a dziko.” Munthu wa Mzimu Woyera, Mulungu, kubwerera mu mawonekedwe amene Iye... Yesu anati, “Ine ndinabwera kuchokera kwa Mulungu; ine ndikupita kwa Mulungu.” Iye anabwera kuchokera ku Muyaya, anadzaponda pansi mu nthawi; anachokamo mu nthawi, kubwerera mu Muyaya.

<sup>36</sup> Ndipo dziko silinamudziwe Iye ayi. “Iye anali mu dziko, dziko linapangidwa ndi Iye, ndipo dziko silinamudziwe Iye ayi. Koma onse amene anamulandira Iye, iwo... anawapatsa iwo mphamvu ya kukhala ana a Mulungu.

<sup>37</sup> Ndipo, tsopano, tsopano Yesu Khristu ali ndi ife, “Komabe kanthawi pang’ono ndipo dziko silidzandiwonanso Ine, komabe inu mudzandiwona Ine.” Tsopano padzakhala dziko limene silikukhoza kumuwona Iye, ndipo padzakhala “inu” amene akukhoza kumuwona. “Pakuti Ine...” “Ine” ndi puronauni yaumwini. “Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, mpaka ku mapeto a dziko.” Ndipo inu, wokhulupirira, adzamuwona Iye mpaka ku mapeto a dziko.

<sup>38</sup> Ahebri 13:8, anati, “Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse.” Mpenyeni Iye mu mphamvu Zake, Ambuye Yesu yemweyo, chikondi chomwecho, zodabwitsa zomwezo, zizindikiro zomwezo zimene zinkamutsata Iye, kusunthirabe mpaka pansi. Iye ali mu Thupi lachinsinsi tsopano, Thupi la iwo owukitsidwawo, kuchoka ku tchimo kupita ku Moyo. Iye akukhala mwa iwo.

<sup>39</sup> Mulungu mu Ulemerero Wake waukulu, Mulungu kudzichepetsa, kubwera kuchokera ku Lawi la Moto, palibe munthu akanakhoza kulikhudza, kutsikira mu mawonekedwe a mnofu wa munthu kumene iye akanakhoza kukhudza, koma Iye anabadwa kwa namwali. Ndiye, kunja uko, kupereka moyo Wake kuti apachikidwe, kuti amuyeretse munthu wochimwa, ndi kuti Iye akhoze kumakhala pakati pa anthu pomwe. Ndi chikondi chotani chimene Mulungu ali nacho kwa munthu, kuti Iye anadzifutukulira Iyemwini pansi, kuti akapange njira yotsukidwa kuti Iye akanakhoza kukhala ndi kumakonda pakati pa amuna ndi akazi. Ndi zokongola. Inde. Ndiwo Atate athu.

<sup>40</sup> Titati ife tiyankhule kwa Iye basi tsopano, Mlembi wa Bukhuli, ife tisanatsegule masamba.

<sup>41</sup> Atate athu Akumwamba achifundo, ife tikubwera kwa Inu, usikuuno, mu njira imene yalonjezedwa kwa ife, “Ngati inu mundifunsa Ine chirichonse mu Dzina Langa, icho Ine

ndidzachichita.” Koteru ife tiribe chilungamo, ife tiribe chirichonse chimene ife tingakhoze kupereka, kokha ife tikubwera mu Dzina la Ambuye Yesu, kudziwa kuti Inu munalonjeza kuti mumva kupyolera mu Dzina limeneli.

<sup>42</sup> Ndiye ife tikukupemphani Inu, podziwa kuti ife tiri nalo pano, pansu pa kuganizira usikuuno, limodzi la maphunziro opambana kwambiri a tsikuli, *Chisindikizo Cha Mulungu*. Atate, ife tikupemphera, Ambuye, podziwa kuti gulu laling’ono ili la anthu limene lasonkhano pano, ngati ine nditi ndiwasocheretse iwo, ine ndidzapereka kufotokoza kwa izo pa Tsiku la Chiweruzo. Ndipo usiku watha, pa, *Chilemba Cha Chirombo*. O Atate, ife tikupemphera kuti Inu mutilondolere ife ndi kutsogolera Mawu amenewo. Musalole kuti Iwo abwerere opanda ntchito, koma mulole Iwo akwaniritse icho chimene Iwo analingilidwira pamene Iwo ankalembedwa mu Bukhu.

<sup>43</sup> Ndipo tsopano bwerani, Mmodzi Woyera, tengani Mawu a Mulungu kuchokera mu Baibulo mmene, ayankhuleni Iwo kupyolera mu milomo ya chivundi, kupita ku makutu achivundi, ndipo mudule onse oyankhula ndi kumvetsera, kuti ife tikakhoze kukwaniritisa chinachake mwa kusonkhana pamodzi uku, usikuuno; podziwa kuti mwina pakhoza kukhala ena pano, ngati dziko litaima chaka china, ati asadzakhale zivundi pa dziko lapansi.

<sup>44</sup> Ndipo tsopano ife tiri ku nyumba ya kukonzedwa, ku nyumba ya Mulungu, kumene ife tiri oti tiyime kuti tikonzedwe. Ndipo mulole Mzimu Woyera undikonze ine, ndi kutseka kamwa yanga, monga Inu munachitira kamwa ya mkango, ndi Daniele. Ndipo Inu mukuwudziwa mtima wanga, ngati mawu amodzi ine ndingati ndiyankhule mosiyana kapena mwa inemwini. Mulole Mzimu Woyera udzoze Mawu aliwonse. Ndingoima ngati chotengera chopandamo kanthu; ndipo mulole Iye ayankhule Mawu a Mulungu, usikuuno, chifukwa mitima yathu ya njala ikuyembekezera kumvetsera kuchokera kwa Iye. Ndipo mulole Iye, Yemwe analemba Baibulo, abwere ndi kuwatanthauzira Iwo kwa antchito Anu odzichepetsa pano. Ife tikupempha mu Dzina la Yesu. Amen.

<sup>45</sup> Tsopano kwa maziko pang’ono chabe, kuti tiyambirepo usikuuno, ndi, *Chisindikizo Cha Mulungu*.

<sup>46</sup> Musati muyiwale, mawa usiku, ife tikufuna inu kuti mutenge funso lanu. Ndi kulilemba ilo momveka, ndi kuliyika ilo pa nsanja, molawirira, kapena pa guwa, molawirira monga inu mungathere. Tsopano phunziro lalikulu ili limene ife tinali nalo usiku watha . . .

<sup>47</sup> Usiku woyamba, usanabwere wathawu, unali Mpingo ndi m’badwo wa mpingo, momwe kuti ife tinamuwonera Yesu ataima pakati pa Zoikaponyali Zagolide Zisanu ndi ziwiri, woti ukamamuyang’ana ngati mwala wa jasi ndi sardiyo, chiyambi



ndi mapeto, Rubeni ndi Benjimini. Kuwona zoyikapomiyuni zisanu ndi ziwiri, kapena zoyimikaponyali zisanu ndi ziwiri zitaima, ndi utawaleza pamwamba pa izo, ngati pangano, ndi momwe Iye anali kuwonekera. Ndipo Liwu Lake linali Liwu la madzi ambiri, zonse Khristu ndi Mpingo, kuyankhula limodzi; ali ndi chomangira cha golide kuzungulira cha ku mbali ya chifuwa cha Mpingo, utaphimbidwa, kugwirizira, Uthenga kugwirizira chilungamo cha Khristu pa Mpingo. Utayima pa maziko a mkuwa, chiweruzo Chaumulungu; Mulungu anatsanulira chiweruzo Chake Chaumulungu pa Khristu, ndipo Iye anazunzika, wosalakwa chifukwa cha wochimwa.

<sup>48</sup> Ndiye, kuwona momwe izo zinayambira ndi mpingo wa Efeso; kenako m'badwo wa mpingo wachiwiri; m'badwo wa mpingo wachitatu; m'badwo wa mpingo wachinai, zaka mazana khumi ndi asanu a mibadwo ya mdima; mpaka kupyola M'badwo wa Lutera; ndi M'badwo wa Filadefiya; ndipo mpaka kufika mu M'badwo wa Laodikaya, m'badwo wotsiriza.

<sup>49</sup> Kuwona mu Chipangano Chakale, momwe iyo inayimidwiridwa mwangwiro pachiyambi, mwa Solomoni, mpaka uko kupyola mu nthawi ya Ahabu, m'badwo wa mdima. Ndipo tinapeza kuti, monga Yezebeli, Ahabu, mlaliki wa mzere wammalire, kapena munthu amene anali wosinthasinha. Monga ngati ochuluka a mamembala ofunda a mpingo lero, anthu, osinthasinha; mu mpingo lero, mawa iwe ukhoza kuwayembekezera iwo kulikonse; akunyengerera, akulekerera, akupita ndi dziko, komabe nkumadzitcha okha Akhristu. Ndipo Ahabu, mu chikhalidwe chimenecho, anagwa chifukwa cha mkazi wamng'ono wokongola, ngakhale mthakati monga onse amatulukira kunja. Ndipo anamukwatira iye, ndipo anabweretsa kupembedza mafano kulowa mu Israeli, mu nthawi ya mdima kumene ya Israeli, m'badwo wa mdima. Tsopano, ife tinapeza kuti iwo anatuluka kunja uko ndi mayimidwe a mkuwa, ndipo mpakanabe, ndipo potsiriza ofunda, uko mpaka Mulungu anawalavula iwo kuchoka mkamwa Mwake ndi kuwalandira Amitundu.

<sup>50</sup> Ndipo tsopano ife tikupeza kuti iwo anayambira ku woyamba, Mpingo wa—wa Efeso, mu kuyambirira, mu m'badwo wa mpingo; m'badwo wa mpingo wotsatira unayamba kuzirala ndi kukhala wofunda; kumapitirira mkati, ndi m'badwo wa mdima. Ndipo basi monga—monga tsiku lija, Ahabu kukwatira wopembedza mafano, Yezebeli, ndi kubweretsa kupembedza mafano mu Israeli; ndiye Chiprotestanti chinakwatira Chiroma, Chikatolika, ndi kubweretsa kupembedza mafano mu mpingo. Kutuluka kupyolera mwa Marteni Lutera; mpaka kupyolera mwa Joni Wesile; mpaka kupita ku Pentekoste; ndi kutuluka, ngakhale kulavulidwa kuchoka mkamwa mwa Mulungu; ndipo Mulungu akutembenukira kwa Myuda kachiwiri, basi mwangwiro.

<sup>51</sup> Tsopano, ine ndikudziwa ine ndiri. . . Inu mukuti, tsopano, ine ndine wofanizitsa. Uko nkulondola. Chifukwa, ine ndikudziwa, ine ndikudziwa chinthu chimodzi, ngati ine ndikupita cha ku mthunzi wanga ndipo ine ndikawona chimene mthunzi wanga momwe ukuwonekera, ine ndiri nalo lingaliro linalake la momwe ine ndimawonekera; kaya ndine chinyama cha miyendo inayi, kapena mbalame ya nthenga, kapena chirichonse chimene icho chiri, chichita mthunzi.

<sup>52</sup> Ndipo Chipangano Chakale chinali mthunzi wa Chatsopano. Ife tinatenga izo usiku watha, mu Chivumbulutso 12, mkazi ali ndi lamulo pansu pa mapazi ake, mwezi ndi dzuwa pa mutu wake, ndi choyimira. Momwe, zinthu zonse izo, Ahebri mutu wa 11 amatiuza ife, izo zonse zinali zoyimira ndi mthunzi. Ine ndikukhulupirira, Ahebri 12, anati iye, “Powona kuti ife tazingidwa ndi khamu lalikulu chotere la mboni, tiyeni ife tiike kumbali cholemetisa chirichonse, ndi tchimo limene limatifooketsa ife mophweka, kuti ife tikakhoze kuthamanga ndi chipiriro liwiro limene layikidwa patsogolo pathu.” Tsopano, ife tinawona zinthu zimenezo. Ndiye usiku watha. . .

<sup>53</sup> Ife tinazitengera mmwamba kumbuyo kuno, kuti tipeze, kapena—kapena, usiku usanafike wathawu. Ife tinapeza ndiye, kuti, mpingo woyamba, momwe iwo unayambira. Iwo unatsegulidwa ndi kuyamba pa Tsiku la Pentekoste, pamene Mzimu Woyera unatsanuliridwa pa okhulupirira. Ndipo ife tinawona kuchitapo kwa okhulupirira awa, ndi momwe Iwo unachitira pa iwo, ndi chimene iwo anachita, ndi zizindikiro ndi zodabwitsa zimene zinawatsatira iwo.

<sup>54</sup> Ndiye ife tikupeza, pa kutseka pa m’badwo wa mpingo umenewo, pafupi zaka mazana atatu, iwo anaphukiritsa chisokonezo pakati pawo, chotchedwa, “chiphunzitso cha—cha Chinikolai.” Ndiye ife tinapeza kuti, icho chinali “ntchito,” poyamba nacho.

Mu m’badwo wa mpingo wotsatira, icho chinadzakhala “chiphunzitso.”

Ndipo kenako nkukhala “chizunzo,” mu m’badwo wa mdima.

<sup>55</sup> Ndiyeno kutulukira pa mbali inayo, cha kuno, ndi kupeza kuti icho chinafungatiridwa kumene ndi mipingo ya Chiprotestanti imene inatulukamo.

<sup>56</sup> Ndiye ife tikubwerera mmbuyo kachiwiri kano ndi kukapeza momwe kufunda konse kuli cha kuno mu mapeto a m’badwo, pa mbali *iyi*, momwe izo zonse zikuzilarira. Monga ngati izo zinachitira pansu pa Ayuda, chotero izo zikuchita pansu pa Amitundu; kuzilara mopita pamene izo zikupita njira *iyi*, mthunzi, kumathima.

<sup>57</sup> Monga ngati izo zinali, masiku a Wesile, ndipo ife tinabweretsa izo mmenemo usiku watha, ndi Lutera. Ndi

chitsitsimutso chachikulu bwanji chimene inu munali nacho, koma, kuzungulira kotsatira, icho chinayamba kuzilara. Kuzungulira kotsatira, icho chinafunda. Ndipo tsopano ndi mulu chabe wa zikhulupiriro ndi mawonekedwe. Ndizo zonse zimene ziripo kwa icho. Mwaona? Ndipo motero ndi momwe izo zakhallira njira yonse konseko. Kotero ndiye ife taphunzitsa zimenezo.

<sup>58</sup> Tsopano, mwatcheru tsopano, mvetserani, kotero kuti inu mukhale mukukumbukira motsimikiza. Ine sindikuwatsutsa anthu Achikatolika, ndipo ine sindikuwatsutsa anthu Achiprotestanti, chifukwa kuchokera kwa onsewo ndi onse a iwo kukubwera Mbewu ya Mulungu, mwa kusankha. Iwo amene anadziwidwiratu ku Moyo adzakupenya Iko ndi kuyenda mwa Iko. Iwo amene sangakhoze kupenya, aziyenda mu mdima. Izo ziri kwa Mulungu. Mulungu amachita zimenezo. Iye analumbira ndipo anamulonjeza Abrahamu kuti Iye adzamupulumutsa iye ndi Mbewu yake. Tsopano, ngati inu muli nayo Mbewu ya Abrahamu, inu muli nawo Moyo Wamuyaya, ndizo zonse, ndipo ndinu olowa mnyumba malingana ndi lonjezo. Ndipo ndizo zonse mwa chisomo ndi mwa kusankha kwa Mulungu.

<sup>59</sup> Tsopano zindikirani, mu izi pano. Ndipo ine ndine basi nthawizina. . . mwinamwake ngati ine ndalalikira mochuluka, kapena kuphunzitsa mochuluka. Izo zakhala zaka. Uwu ndi msonkhano wophunzitsa woyamba umene ine ndakhalapo nawo, kwa pafupi zaka zisanu ndi zitatu. Ndipo uli chabe pang’ono, mwinamwake dzimbiri pang’ono pa iwo, mu malo. Nthawi iliyonse imene inu muli—inu muli. . . Ndifunsemi ine funso lililonse limene inu mukufuna kufunsa; liyikeni ilo pa nsanja, kapena paguwa, ndipo ine ndidzakhala wokondwera kulitenga ilo.

<sup>60</sup> Tsopano zindikirani. Koma zonse zimene ine ndikudziwa za Ilo, ine sindinaphunzire Izo ndi munthu, mwa seminare. Ine ndapemphera mpaka ine nditakhala nalo vumbulutso la izo, ndipo izo zimayenera kufanizana ndi Mawu a Mulungu.

<sup>61</sup> Mu Chipangano Chakale, iwo anali ndi njira zitatu zodziwira uthenga. Njira yoyamba imene iwo amapezera, izo zinali kapena zitalembedwa pa lamulo; chinthu chotsatira chinali mneneri; kapena chinthu chotsatira chinali Urimu Tumimu. Tsopano mphunzitsi aliyense amadziwa chimene Urimu Tumimu anali. Iko kunali—kuwala kumene kunkawala pa chapachifuwa cha Aaroni, chimene iwo anali nacho chitapachikidwa mu kachisi. Tsopano, ngati mneneri ananenera, ndipo Kuwala osakhoza kuwalira pa Urimu Tumimu, izo zinali zolakwika. Ilo linali yankho Laumulungu la Mulungu, “Izo zinali zolakwika.” Ndiye ngati iwo. . . Ngati wolota alota loto, ndipo ilo silinawalire pa Urimu Tumimu, ilo linali lolakwika.

<sup>62</sup> Tsopano, Urimu Tumimu wafika pothana naye, mwa lingaliro limenelo, koma *Iyi* ndi Urimu Tumimu ya Mulungu tsopano, Baibulo. Ngati mneneri, kapena wolota, kapena chirichonse chimene chiri, kapena mphunzitsi, sanakhazikitse zamulungu zake chimodzimidzi pa PAKUTI ATERO AMBUYE, ine sindizikhulupirira izo, mwaona. Izo ziyenera kubwera momwemu *Umu*, kuchokera ku Genesis mpaka ku Chivumbulutso, osati mu malo amodzi chabe. Izo ziyenera kubwera kupyolera mu Baibulo ndi kulimangiriza Ilo chimodzimidzi palimodzi. Inde, bwana. Izo ziyenera kufanana ndi lonse la Ilo, ndipo litakolowedwa Ilo lonse palimodzi. Ngati iwe sutero, iwe ukhoza kutenga chinthu chimodzi ndi kunena kuti ameneyo ndi purigatorio, ndi kulalikira Chikatolika kuchokera mu Baibulo. Koma izo ziyenera kugwirizana mwathunthu kuchokera ku Genesis mpaka ku Chivumbulutso, kupangitsa chithunzicho kumveka. Ndiko kulondola.

<sup>63</sup> Ndipo Mzimu Woyera uli Umodzi Umene umakutsukirani inu chithunzi Ichi, ngati inu mutangomulola Iye kuti achite izo. Iye adzakutsegolerani inu mu Kuwala konse. Baibulo linanena chomwecho. Yesu anati Iye adzachita izo.

<sup>64</sup> Tsopano zindikirani pamene...Kachiwiri, tsopano, ife tikupeza chimene iwo anachita uko. Ndiye, patapita kanthawi, iwo anali ndi chiphunzitso. Iwo anali ndi kuzunza. Iwo anatulukuka.

<sup>65</sup> Ndiyeno ife tinabwera nkudzapeza kuti, kuti mu tsiku lino tsopano, kuti Baibulo linaneneratu kuti padzakhala nthawi imene anthu ati adzalandire chilemba, ndipo chilemba cha chirombo.

<sup>66</sup> Nthawi iliyonse pakakhala kenakake kakang'ono kakuwuluka mu dziko, aliyense amati, “Ndicho chilemba cha chirombo.” Pamene akale...Ine ndinali nditadzedwa kumene mu mpingo wa Baptisti, pamene ine ndinamva za N.R.A. Chabwino, aliyense anati, “Ndicho chilemba cha chirombo.” Ndiyeno chirichonse chikayambika motsatira, “Ndicho chilemba cha chirombo.”

<sup>67</sup> Ndipo tsopano iwo amati, “Apa pakubwera Russia uko, chikomisini, ndi chilemba cha chirombo.” Koma, ndi bodza. Icho si chilemba cha chirombo. Baibulo limatiuza chimene chilemba cha chirombo chiri. Chilemba cha chirombo si chachikulu chotsutsa-chipembedzo chotsutsa-dziko chitawuka monga choncho. Chikomisini si Russia; chikomisini ndi mzimu. Ndizo zonse. . . Ife tisati—tisati tizidandaula ndi Russia.

<sup>68</sup> Kuvunda kwathu komwe ndi kumene kukutipha ife. Chikomisini chikusuntha pakati pomwe pa mipingo yathu ndi china chirichonse, inu mukudziwa zimenezo, mu masukulu athu, mu makomo mwathu, kulikonse, mu fuko lathu. Chinthu chonsecho chiri basi nchodyedwa ndi mbozi. Phwithi akujompha

pa apulo samaliwononga ilo; ndi mbozi pa chirikati imene imawononga apulo. Ndicho chimene chiri, ndi kuvunda chabe pakati pa ifeeni. Kumapita, kumadzitcha tokha Akhristu, ndi kumachita monga dziko, ndi kumavala monga dziko, ndi kumatengera za dziko, ndi kumadzitcha tokha... Dziko likudwala ndi kutopa ndi zoterozo. Ndipo si dziko lokha, ambiri a Akhristu ali, nawonso. Inde.

<sup>69</sup> Ine kawiri kawiri ndanenapo kuti, “Mulungu athandizire tsiku limene anthu ati adzakhale chimene iwo ayenera kukhala. Ngati ine ndikanakhala womutsutsa Iye, ine ndikananena kuti ine ndinali womutsutsa Iye, ine ndikanakhala womutsutsa Iye mu chirichonse chimene ine ndikanakhoza kukhala.” Koma ine ndine wa Iye, ndipo ine ndimamukonda Iye, ndipo ine ndimamukhulupirira Iye. Ndipo—ndipo moyo wanga uli mu manja Ake, kuti achite nawo chirichonse chimene Iye akufuna kuchita, chifukwa ine ndikukhulupirira kuti Chikhristu ndi Choonadi. Ndiko kulondola. Ine ndikukhulupirira kuti ndicho Choonadi.

<sup>70</sup> Pa kuyenda mu dziko, ndi kuli yang’ana ilo lonse mu timalingaliro tosiyana, ndi zina zotero, oyambitsa awo onse anafa ndipo akugona mmanda, ndipo iwo ali nazo zamulungu. Ndimo basi momwe mpingo wa Chikhristu umapita nalo ilo, ngakhale.

<sup>71</sup> “Koma iwo amene akumudziwa Mulungu wawo adzachita zazikulu.” Ndipo Mphamvu ya chiwukitsiro cha Yesu Khristu imakhala mwa munthu. [M’bale Branham agogoda pa guwa kasanu ndi kamodzi—Mkonzi.] Ndiko kulondola. Iye sali wakufa; Iye ali wouka. “Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, ndipo zinthu zimene Ine ndichita inu mudzazichitanso.” Inde, bwana.

<sup>72</sup> Ndiye dziko limayang’ana panja ndi kunena, “Zotentheka.” Inu munawona pamene ife tinazitenga izo usiku watha, mwa kuthandiza kwa Mulungu.

<sup>73</sup> Tsopano, ife tikupezapo kuti chinthu choyamba chimene chinayamba chawukapo kuti chipange mawonekedwe aliwonse a chirombo, konse, kapena... *Chirombo* chimatanthauza “mphamvu.” Ife tinapita kupyola mu zophiphiritsa zonse ndi chirichonse usiku watha, kuti titsimikizire kuti chirombo chinali mphamvu. Ndipo icho sichinabwere kuchokera ku Russia. Icho chinabwera kuchokera ku Roma. Ndiko kulondola. Icho chinabwera kuchokera ku Roma.

<sup>74</sup> Ndipo ilo silinali—ilo silinali gulu la anthu. Ilo silinali bungwe landale. Iko kanali kakhazikitsidwe kachipembedzo. Iwo unali mpingo umene “ukukhala pa mapiri asanu ndi awiri,” ndi mwamuna mmodzi yemwe anali ndi mphamvu zolamulira pa dziko lonse, mkati mmenemo. Kulondola chimodzimidzi. Ndipo ife tinapeza kuti uwo unali mkazi, ndi kumujambula iye

momveka basi. Osati kutenga kutanthauzira kwanga kwanga; kuwerenga Baibulo basi. Kuti, palibe malo ena mu dziko, palibe mzinda wina mu dziko, umene umalamulira pa dziko lonse. Mu fuko lililonse, msempha uja wa Chiroma ukuyenderera ngati mu zala zakuphazi khumi za masomphenya a Daniele, ndipo ife tikupeza kuti umenewo unali Mzinda wa Vatikani.

<sup>75</sup> Pafupi dazeni la Akatolika odzipereka atakhala muno usiku watha. Iwo anakhala duu ndipo amamvetsera. Iwo ali odzipereka. Iwo ali ndi njala.

<sup>76</sup> Tsopano, inu simungatsutsane ndi wansembe. Iye sangatsutsike, chifukwa, wansembe, “Ngati mpingo unena chirichonse chosiyana kwa Baibulo ili, mpingo ukulondola.” Kwa ine, Baibulo likulondola ndipo mpingo ukulakwitsa. Mwaona? Inu simungatsutsane nawo iwo. Iwo, inu muli... Apo palibe njira yotsutsirana. Apo palibe njira yokambirana kapena kutsutsirana. Chifukwa, iwo amakhulupirira, “Chimene mpingo unena, ndi chimenecho! Ndi chimenecho, chimene mpingo unena, ziribe kanthu kaya Baibulo linene chiyani. Ndi chimene mpingo unena!” Iwo amakhulupirira mpingo. Ife timakhulupirira Baibulo.

<sup>77</sup> Tsopano ife tikupeza kuti iwo unali kutchewa... Mpingo unali mkazi. Ndipo iwo unali kutchewa mwachimvekere, liwu loyipa la “HULE,” ndiyeno iwo unali “MAYI WA TIMAHULE.” Ndipo ife tinapeza kuti mpingo wa Katolika unali woyamba manthu wa mpingo. Iwo uli chimodzimodzi chimene iwo unati unali. Iwo uli mpingo woyamba kuti ukhale konse bungwe. Pamene Mulungu anapanga konse bungwe chipembedzo, iwo unali mpingo wa Katolika. Bungwe loyamba limene linapangidwapo bungwe mu dziko, la chipembedzo cha Chikhristu, mpingo wa Katolika. Tsopano...

<sup>78</sup> Ndiyeno, potsiriza, iwo unali “MAYI WA TIMAHULE.” Iwo unapereka kubadwa kwa mipingo, pambuyo pa iwowo, chifukwa iwo sakanakhoza kukhala anyamata. Iwo amayenera kukhala asungwana, ndipo ife tinapeza kuti mpingo wa Chiprotestanti ndi chotuluka ku mpingo wa Katolika. Mwa kufufuza Malemba, ndipo yang’anani pa bukhu lanu la mbiriyakale, ife tikuwona kuti mpingo wa Chiprotestanti ndi chotuluka. Ndipo Achiprotestanti sangakhoze kufuula pa Akatolika, chifukwa, onsewo, amanena kuti iwo ali “TIMAHULE” ndi “HULE.” Ndizo mosabisa, koma ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE. Ndiko kulondola.

<sup>79</sup> Penyani, ndiye iye anati, “Tiyeni ife,” mu United States, iwo anati, “tiyeni ife tipange fano kwa chirombo.” Ngati chirombo chinali mphamvu, ndipo mphamvuyo inali bungwe; osati kutenga zamulungu tsopano. Ndiwo Mawu a Mulungu. Bungwe la mpingo wa Katolika linadzipanga lokha bungwe limodzi ndipo linapanga chi-... kugwirizana. Ndipo iwo anakhazikitsa,

chimene iwo amachitcha, “makolo oyambirira” limodzi, ndipo anapanga bungwe mpingo wa Katolika, ndipo anapanga m—m—m—mwambo, ndi chimene iwo anakhulupirira ndi chimene iwo akanati aziphunzitsa, chikhulupiriro cha konsekonse. Ndipo iwo anakakamizira icho kwa anthu, mwa chilango.

<sup>80</sup> Ndiyeno pamene Marteni Lutera anatulukamo, powona Mzimu wa Mulungu ukumutsogolera iye kuti atuluke. Mmallo mowalola anthu kuti akhale afulu, iye anaupanga bungwe mpingo; fano lofanizidwa kwa chirombo, mphamvu yandale yofanizidwa kwa icho. Mmallo mowalola anthu kuti aziyenda monga Mulungu akuperekera kuwala, iwo anachita bungwe pansi pa kusunga mwambo, ndipo iwo anayenera kukhala mu kusunga mwambo kumeneko.

<sup>81</sup> Mulungu anasunthira kumene kulowa mu mpingo wa Methodisti. Achimethositi anali nacho chitsitsimutso chimene chinasesa dziko; Mzimu Woyera uli ndi iwo, akuphunzitsa kuyeretsewa. Ndipo chinthu choyamba inu mukudziwa, pamene iwo anachita izo, ndiye iwo anaupanga bungwe mpingo, anapanga fano kwa chirombo, ndiko kulondola, mphamvu zandale, zachibungwe, kuwamangirira anthu a Mulungu ku chikhulupiriro; mmalo mokhala afulu kuti azipembedza ndi kuyenda mu kuwala pamene kuwala kunawonetsedwa pa njira zawo.

<sup>82</sup> Iwo anawaika iwo kumbuyo, mu m’badwo umenewo. Uko kunali kuwala kwabwino kumeneko. Uko kunali kuwala kwa—kwa mpingo wa Pergamo.

<sup>83</sup> Koma nanga bwanji mpingo wa Filadefiya? Ndiko kuwala kwina. Koma, inu mukuona, ziribe kanthu kuti iwo anachita bungwe chotani, Mulungu anasunthira kumene mu m’badwo *wu* wa mpingo, mulimonse, anatumizako munthu, wa dzina la Joni Wesile. Lutera sakanakhoza kutsatira iko, chifukwa iye samakuhulupirira iko. Iye anali atachita kale bungwe kumbuyo *kuno*.

<sup>84</sup> Ndiye Joni Wesile anachita bungwe mothinita kwambiri, ndipo anafika pa malo. Iyo inali nthawi kuti m’badwo wa mpingo *wu* kuti ubwere mkati. Mulungu anatumiza gulu la Chipentekoste; kupita kunja kuno ndi ubatizo wa Mzimu Woyera. O, Amethodisti anati, “A-o. Ha! Ife sitingakhoze kupita ndi Zimenezo. U-nhu! Ife sitimakhulupirira mu zinthu zimenezo. O, ayi.” Chifukwa chiyani? *Uku* ndi kuwala kumene iwo anali kuyendamo, *apa*; *pano* pali kuwala kwa cha *kuno* tsopano.

<sup>85</sup> Ife tikupitirira patsogolo kumka kokalowa kwa dzuwa. Kumbukirani chimene mneneri ananena? “Ilo lidzakhala tsiku limene liti lidzakhale lamitambo, osati usiku kapena masana, koma madzulo iko kudzakhala Kuwala.” Kuwala kumene kunawalirapo kamodzi mu dziko lakummawa kwa Myuda, mu

la akummawa (Ayuda ali anthu akummawa), Iko kukuwalira pa Amitundu; Kuwala komweko, Mzimu Woyera womwewo, mu masiku otsiriza cha kuno, ubatizo womwewo wa Mzimu. Ife takhala tikupyola mibadwo yonse iyi kupyola pano, kumene kulibe Kuwala ngakhale nthawi ya mdima, koma la mitambo, tsiku lolunda; koma pomwe *apa*, monga Kuwala kunawalira basi mofanana monga iko kunachitira kumeneko.

<sup>86</sup> Ndicho chifukwa, “Iye ali woti ukamamuyang’ana monga jaspi ndi mwala wa sardiyo; Alfa, Omega, Chiyambi ndi Mapeto; Iye Amene Analiko, Amene Alipo, ndipo Ati Adzabwere; Muzu ndi Mphukira ya Davide; Nyenyezi ya Mwawa.” Apo izo ziri. [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] Ine ndikuyembekeza inu mukuziona izo.

<sup>87</sup> Ndipo, kumbukirani, kuti ife tinapeza, popanda kulakwitsa kumodzi, kuti chilemba cha chirombo ndi chilemba cha chinyengo, awo ali, mamembala a mpingo okanirira ku mpingo wawo mmalo mwa kuyenda mu Kuwala. Iwo amakukana Kuwala, ndipo palibe kanthu katsalira koma mdima. Ndiko kulondola, onse Achikatolika ndi Achiprotestanti. Apo pali “chirombo, ndi hule,” ndipo iye ali ndi ana aakazi “kahule”. Ndipo ana aakazi auhule awa, pamene iwo anatulukira, iwo anali namwali kuchokera mu Kuwala kwa tsiku limenelo, ndipo iwo anapanga bungwe ndi kumawabweretsa anthu pansi apa, kubwerera umu, kuwapanga iwo mtundu womwewo wa chinthu chimene Roma anali pachiyambi. Baibulo linanena chomwecho. “Chirombo; ndi fano kwa chirombo; lembo la dzina lake,” ndi zina zotero.

<sup>88</sup> Momwe ife tinapyolera mu chinthu chonsecho, usiku watha, ndipo Baibulo mwachimvekere...osati zoyankhula za winawake. Koma Baibulo linaziyala izo apo, kuti cha mitu isanu ndi iwiri, chirombo cha nyanga khumi chinabwera [Malo osajambulika otheke pa tepi—Mkonzi.] kuchokera ku Roma, chinali uko ku Roma, ndipo chinali “Iye amene analiko, amene kulibe; ndipo amene aliko, ndi amene kulibe,” papa mmodzi pambuyo pa mzake, papa mmodzi pambuyo pa mzake, ndipo adzapita mpaka mu chitayiko. Ndi kupeza kuti mkazi wakale yemweyo anabala asungwana ena. Iwo anali namwali kuchokera pachiyambi, anayenda mu Kuwala kumene iwo anali nako. Ndiyeno iwo anayamba kuchita ngati timahule, ndi kupita kumbuyo komwe akuchita chinthu chomwecho chimene mayi wawo amachita. [M’bale Branham agogoda pa guwa kawiri.] Chimodzimodzi. Chimodzimodzi.

<sup>89</sup> Ndiroleni ine ndikuuzeni inu chinachake, akazi. Mvetserani. Inu mwina simungakhale nako kudalira kochulukira chotero mwa ine tsopano, pamene ine ndikuphulitsa zinthu izi. Ndipo izo si kuti ndikupwetekeni inu; ndi kuti ndikuthandizeni inu. [Osonkhana anena, “Ameni.”—Mkonzi.] Koma pamene inu mukuwawona anthu, mipingo lero, ikuloleza akazi



awo...Tsopano, ine—ine ndifika kwa amuna, nawonso. Koma kumawaloleza akazi awo kuti azichita momwe iwo amachitira lero, ndipo iwo nkumadzinenera Chikristu! Ine sindikukutsutsani inu akazi; ine nditero, ukatha usikuuno. Koma, penyani, ine—ine sindikukutsutsani inu akazi tsopano. Koma, mlongo wanga, ochuluka a aphunzitsi awa a ku seminare kuno, kapena aphunzitsi a kumanda, kapena chirichonse chimene inu mumachitcha icho, ochokera kuno kwinakwake, akungokulolani inu kuyenda mu zinyengo zimenezo. Baibulo linati, “Iwo anali akhungu, akutsogolera akhungu.” Ndizo zoon. Tsopano . . .

<sup>90</sup> Ndipo, Yesu, powona izi, ndipo podziwa kuti ina ya mipingo ya Chiprotestanti iyi idzayenda molunjika kumene mpaka ku chipata cha Kuwala, ndi kupotoloka kuchokako. Yesu, mu Mateyu 24:24, ananena kuti izo zidzakhala chomwecho, “Wotsutsakristu adzakhala pafupi kwambiri ngati weniweniyo, mpaka iye akanadzanyenga Wosankhidwa amene, ngati kukanakhala kotheka.”

<sup>91</sup> Tsopano, onani, Chiroma, Chikatolika, o, icho chinawakhoma ena a inu Achiprotestanti pa mutu. Koma, munthu amene ali ndi pang’ono za chisomo iye, pang’ono . . . amadziwa pang’ono za Baibulo, iye adzapewa ndi kuchokako. Ndiko kulondola. Kudolola kwake ndi kwakuda kwa iye; iye amadziwa kuti palibe kanthu kwa izo, chinthu chonse icho chimene iwo amaphunzitsa. Palibe Lemba kwa icho; tsopano ndiyeno, iwo amagunda pang’ono pokha.

<sup>92</sup> Bodza lalikulu limene linayamba lanenedwapo, linali ndi Choonadi chochuluka mwa ilo. Ndiko kulondola. Ndipo limodzi loyambalo, Satana akuyankhula kwa Eva, iye ananena Choonadi chochuluka. Koma iye anali ngati, pansu pa izo, iye anali ndi bodza limene linamutsutsa iye, ndi kuwononga m’badwo wonsewo, chirengedwe chonse. Ndiko kulondola.

<sup>93</sup> Inu muyenera kusamala izo. Izo ziyenera kubwera Choonadi *apa* ndi Choonadi *pano*, Choonadi *apa* ndi Choonadi *apo*. Kugunda kulikonse kwa izo, Choonadi; kundanda mofanana, njira yonse mopyola.

<sup>94</sup> Ndiyeno momwe anthu angakhoze kuwuwona mpingo woyambirira kumbuyo uko unayatsidwa ndi choyikapomiyuni choyikaponyali, ndiyeno cha *kuno* kuwona chinthu chomwecho chikuchitika chimene chinachitika kumbuyo uko, ndipo Mawu a Mulungu akunena kuti izo zidzakhala “Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero ndi nthawizonse.” Ndipo nkukana izo? Izo zimangosonyeza kuti iwo akukana Kuwala, ndipo akuyenda mu mdima; chinthu chokha chimene chatsalira.

<sup>95</sup> Ndizo zoon, m’bale wanga. Ine sindikunena izo kuti ndikhale wanzeru. Mulungu akudziwa zimenezo. Iye amawudziwa mtima wanga. Ine ndiri nawo utumiki, ndi

zochulukuka patsogolo pangabe. Ndipo podziwa kuti tsiku lina, pa Malo Achiweruzo, ine ndikayankha chifukwa cha zinthu izi. Ndi kulondola chimodzimidzi. Ine ndidzapezeka wotsutsa wabodza, mphunzitsi wabodza, ndiye Mulungu adzanditsutsa ine. Ndiko kulondola. Koma ngati ine nditadziwa Choonadi cha zinthu izi, ndipo nkusakuuzani inu, Iye adzanditsutsa ine ndiye, ndithudi mokwanira.

<sup>96</sup> Ananena kwa mlonda, “Yang’anira! Ngati iwe ulephera kuwachenjeza, ndiye Ine—Ine ndidzafunsa pa dzanja lako. Koma ngati iwe uwachenjeza, ndipo iwo nkumapitirira, iwo adzafa mu tchimo lawo, koma Ine sindidzafunsa izo pa dzanja lako. Iwe udzakhala mfulu.”

<sup>97</sup> Kotero ife tikufuna kukhala osamalitsa kuti tidziwe chimene chiri Choonadi, molingana ndi Baibulo. Ndi momwe m’badwo uwo unayambiramo, ndi chimene iwo anachita, ndipo lero kuwuwona mpingo wa Chiprotestanti pansi kumene chimodzimidzi.

<sup>98</sup> Penyani pano. Iyo inali, nthawi yaitali kale, ndipo inu anthu achiyero, kunali kolakwika kuti inu akazi muzidula tsitsi lanu. Kodi ndi chiyani chinali cholakwika ndi cholondola cha izo? Pamene Baibulo linanena kuti, “Ngati mkazi aliyense adula tsitsi lake, mwamuna wake ali nawo ufulu kuti amupatse iye chisudzulo.” Kuphunzitsa komveka, koma ndilo Baibulo.

<sup>99</sup> Ndipo inu akazi, mumatuluka kunja kuno ndi kumatchetcha bwalo lanu, mutavala ovololo, ndi zovala zachimuna. Ndipo Baibulo linati, Mulungu Wamphamvuzonse anati, “Mkazi yemwe ati adzavale chovala chomwe chiri cha mwamuna, ndi chotembereredwa, chauve pamaso pa Mulungu.” Ndipo inu mumachita izo.

<sup>100</sup> Ndipo inu mumasuta ndudu, inu mumapita ku zovina ndi ziwonetsero, ndi kukhalabe a mpingo. Inu mukusonyeza kuti inu munatenga mtundu wina wa chinachake; inu simunaikidwe chilemba Kumwamba, Mzimu Woyera. Pakapita kanthawi ife tifika mu zimenezo, ndi kukusonyezani inu zosiyana kuposa zimenezo. Tsopano, ndizo chinthu chaching’ono chabe.

<sup>101</sup> Ndipo inu amuna, mumalowa mu mpingo, mukuyenda uko mmisewu ndi ndudu mkamwa mwanu, ngati n—ng’ombe ya ku Texas, yopanda nyanga. Ndi kutenga... Ine sindikunena izo chifukwa cha nthabwala. Ine sindimakhulupirira kuchita nthabwala pa guwa. Ine ndikunena chimene chiri Choonadi. Kupita uko mu msewu, ndi kukakhala mu malo, ndi kumanama, ndi kuba, ndi kunyengezana wina ndi mzake, ndipo ndi madikoni pa bolodi la mpingo.

<sup>102</sup> Kupita uko mu mipingo ndi kukasewera masewero awa amatsenga akale, sindizo kanthu mu dziko koma maula wamba, otsiki-tsitsa. Ndiko kulondola. Ndipo inu mumachita zimenezo, ndiyeno nkumafuula za wopanga mabuku. Inu mulinso basi

oyipa, mu mipingo yanu, inu Amethodisti, Abaptisti, ndi Achipentekoste, aliyense yemwe inu muli amene mumachita zimenezo. Ndiko kulondola. Ndipo inu mukudziwa kuti ndizo zooni. Koma ndi chiyani icho? Inu mumawunjika kumbuyo komwe monga mayi wanu kale kutali. Chimodzimodzi chinthu chomwecho, ndipo mphika sungakhoze kunena ketulo kuda. Ndipo kumeneko kuli mzimu umenewo wa zinthu.

<sup>103</sup> Koma ine sindine kanthu kotsutsa anthu a Chikatolika. Ine sindine kanthu kotsutsa Amethodisti, kapena Abaptisti, kapena Apresbateria. Mulungu ali nawo anthu, Mbewu za Abrahamu, kunjani uko. Si kutsutsa anthuwo ayi. Ndi zokhudza mipingo yawo, kudzipanga bungwe okha kumeneko, ndipo iwo amapembedza mpingo mmalo mwa Mulungu. O, inu Achiprotestanti simukufuna kukhulupirira zimenezo, koma inu mumachita izo, mulimonse. Ine ndinena kuti, kodi ndinu Akhristu?

<sup>104</sup> Chabwino, kuno osati kale litali, M'bale Bosworth anamufunsa msungwana, anati, "Kodi ndinu Mkhristu!"

<sup>105</sup> Iye anati, "Mkhristu? Ine ndikupatsani inu kuti mumvetse, ine ndimayatsa kandulo usiku uliwonse!"

<sup>106</sup> Chabwino, tsopano inu Achiprotestanti mumaganiza kuti ndicho chinachake? Kodi ndinu Mkhristu? "Ine ndikupatsani inu kuti mumvetse, ine ndine wa Methodisti," kapena "wa Baptisti." Chabwino, izo sizikutanthauza kanthu koma inu mwayenda kuchoka ku tsiku la chisomo, mwa inunokha, kwa ine; ndiko kulondola, ngati ndizo zonse zimene inu muli, wa Methodisti basi kapena wa Baptisti. Ngati inu simuli Mkhristu mu mpingo wa Methodisti umenewo, kapena wa Baptisti, kapena wa Katolika, inu ndinu otayika. Ndiko kulondola. Koteru pamene pali chimodzimodzi chilemba chanu.

<sup>107</sup> Zilemba zonsezo ndi zauzimu. Tsopano ine nditsimikizira izo kwa inu mwa Baibulo. Zilemba zonsezo ndi zilemba zauzimu.

<sup>108</sup> Anthu ambiri amaganiza, "Two adzachita kuti umke uko nakakudinda nchome wa chinachake pa mphumi yako, kudinda chinachake mu dzanja lako." Ife tinapeza, usiku watha, ilo linali bodza. Inde, bwana. Ndiko kulakwitsa. Ndi chilemba chauzimu. Izo—izo zangobisika. Ndipo, penyani, nthawi zambiri . . .

<sup>109</sup> Tsopano ine ndikudziwa izi zikhoza kukhala zikufwanyula nthenga zochuluka, ndipo izo—izo—izo zikuwoneka zolimba. Koma izo—izo ziwongoka ngati ife tingoti . . . ndi kumupatsa Mulungu mwayi pang'ono. Ine—ine sindikutanthauza kuti ndikhale wamwano, koma ine—ine ndikungoyesera kunena choona, ndi mtima wanga wonse.

<sup>110</sup> Pamene Yesu Khristu anawona mpingo uja wa Chipentekoste ukugwa kuchokera ku mpingo wa Katolika uja kutaliko, ndi kutulukamo ndi kupita molunjika ndithu mmbuyo, ndi kumapotolokera kumbuyo kachiwiri basi monga iwo

anachitira, Iye anati, “Mzimuwo udzakhala pafupi kwambiri, mpaka iwo udzanyenga Osankhidwa amene. . .”

<sup>111</sup> Kodi inu munali kuzindikira, amzanga Achikhristu, kuti wotsutsakhristu, yemwe ali chilemba cha chirombo? Wotsutsakhristu, aliyense amadziwa zimenezo wotsutsakhristu pamenepo, ndicho chilemba chake, chiri. . .za mphamvu yake. Ndipo, onani, ndi chirombo, ndi mphamvu. Pali mphamvu ya mpingo wa Katolika. Pali mphamvu ya mpingo wa Methodist.

<sup>112</sup> Ine ndinapita, kuno osati kale litali, kwa njonda yabwino kwambiri. Ngati ine sindikulakwitsa, iye wakhala momwemuno mu tchalitchi usikuuno. Ndipo Edith Wright wamng’ono ndi iwo anabwera ku msonkhano komwekuno, osakwana mailosi makumi awiri kuchokera pa malo ano. Ndipo, ife, anthu. . . Ine ndinali kulalikira chabe Uthenga wa chipulumutso. Iye anachita kukwera pamwamba pa magalimoto kuti akafike ku malowo. Ndipo usiku umenewo, abusa anandiyitana ine molunjika, anati, “Ine ndiri wachisoni kukuuzani inu, M’busa Branham. Koma iwo anandiuza ine kuti iwo anali ndi anthu ena odwala amene abwera mkati umo, ndipo mwamuna wathu wa mu bomali anabwera mkati ndipo anati, ‘Machiritso Auzimu ayi mu mpingo wa Methodist.’ Koteru inu muyenera kupita pa nsanja, kukadzibalalitsa nokha, ndi kuwasiya osonkhana.” Ndiko kulondola.

<sup>113</sup> Chifukwa chiyani? Mphamvu ya mpingo wa Methodist. Ndiyo mphamvu ya chirombo. Mpingo wa Baptisti mofanana; Achikampubelo, ndi Achilutera, ndi onse a iwo, ndi Achipentekoste, oyipa mofanana. Ndiko kulondola. Ine ndakhalapo nawo anthu Achipentekoste. . .Ndipo a Assemblies of God apita mu bungwe la mipingo, chimene chiri a—a. . . Iwo anangodzokoloweka okha komwe kuno, limodzi ndi “mayi” wakale kahule. Koteru bungwe la mpingo lirilonse likuchokera ku Roma. Uko kuli mayi wa izo. Ndipo ine si woyera wa Tsiku la Masika, kapena Mvula ya Tsiku-Lamasika, kapena chirichonse chimene inu mumachitcha icho. Ine sindikufuna. . .Ine sindine wa chimenecho.

<sup>114</sup> Koma ine ndikutanthauza ichi, kuti amuna ndi akazi ayenera kukhala afulu mwa Khristu Yesu, kuti aziyenda mu Kuwala. Ndipo mpingo uliwonse uyenera kukhala chinthu chomwecho. Ndizo zoon.

<sup>115</sup> Tsopano, zindikirani ichi, momwe Baibulo. . .Mvetsani izo. Bungwe limenelo, kumbukirani, apo ndi pamene ilo lagona, apo pomwe. Ndipo ife tikupeza, kuti pamene mpingo wa Chikatolika unayamba kumbuyo uko, iwo anatenga ubatizo wabodza umene iwo anatuluka nawo, kukonkha mmalo mwa kubatiza. Palibe Lemba limodzi mu Baibulo la zimenezo. Ndipo osati zokhazo basi, koma Mzimu Woyera, ndi ubatizo wa madzi, ndi mawonekedwe, ndi maudingo, ndi china chirichonse,

kungopanga zotonga basi kwa chenichenicho. Ndipo palibe mtumiki mu dziko, yemwe angakhoze kundisonyeza ine malo amodzi pamene izo zinayamba zachitikapo konse mu mpingo woyambirira. Ndiko kulondola. Izo siziri mu Baibulo. Koma iwo anatuluka ndi zimenezo, ndipo ife timagwadira kumene kwa izo. Kodi inu mukuona kumene ife tikupita kumbuyo komweko?

<sup>116</sup> Ndipo lero inu mukudabwa chifukwa chimene ife tiribe chitsitsimutso. Ndi chimenecho chomwe chiri, m'bale. Chimene ife tikusowa lero ndi chabwino, cha nthawi-yakale, chitsitsimutso cha Paulo Woyera, ndi Mzimu Woyera wa m'Baibulo utabwerera mu dziko kachiwiri. Ndicho chimene ife tikusowa. Tsopano . . .

<sup>117</sup> Ndipo iwo atenga “chilemba cha chirombo,” kapena “lembo la dzina lake,” chimene iwo anapangira fano kwa icho. Fanolo linali bungwe basi monga mpingo wa Katolika. Iwo anawupanga bungwe iwo ndipo anapanga fano la mpingo wa Katolika. Kodi mpingo wa Methodisti ndi fano la iwo; mpingo wa Baptisti, mpingo wa Presbateria, mpingo wa Pentekoste, mpingo wa Holiness, Pilgrim Holiness, United Brethren? Uliwonse umene unapanga bungwe, unatengera izo kuchokera kumeneko. Izo munalibe konse mu Baibulo la Mulungu. [M'bale Branham agogoda pa guwa kamodzi—Mkonzi.] Ndiko kulondola. Mabungwe; kupanga bungwe!

<sup>118</sup> Mulungu ndiye mtsogoleri. Tengerani izo kumbuyo motalika mmene inu mukufunira kutero. Yang'anani pa Israeli, akubwera uko kuchokera ku Igupto.

<sup>119</sup> Ndi Amoabu onse awo atayima kumeneko, achikhazikitso, akupereka nsembe; maguwa asanu ndi awiri, zisanu ndi ziwiri mbu. . . nkhosa zisanu ndi ziwiri, kuyankhula za kudza kwa Khristu; ng'ombe zisanu ndi ziwiri, zoperekedwa zoyera. Pomwepo, mneneri wake wamkulu atayima kunja uko, Balaamu, kuti atemberere Israeli. Ndipo uko kunali Israeli. . . Uko kunali Moabu, fuko lalikululu. Uko kunali Aamori ndi onse, fuko lalikululu, anachita bungwe palimodzi ngati fuko.

<sup>120</sup> Ndipo Israeli anabalalika kunja uko ku minda ndi gulu la mahema. Iwo anali “amwendamnjira ndi alendo, akufunafuna Mzinda kuti udze,” mosamalitsa ochokera mzipembedzo. Ndipo kodi iwo anachita chiyani? Iwo anali nazo zizindikiro ndi zodabwitsa zikuwatsatira iwo. Awa analibe; ndipo iwo anali kuchita nsanje kwa awo. Imeneyo inali mizimu.

<sup>121</sup> Mulungu amachotsapo munthu Wake, koma osati Mzimu Wake. Iye anamutenga Eliya, ndipo Mzimu Wake unabwera pa Elisha; zaka mazana angapo kenako, iwo unabwera pa Yohane M'batizi; unanenedweratu kachiwiri mu tsiku lotsiriza.

<sup>122</sup> Mdierekezi amatengera khalidwe lake, koma osati mzimu wake. Mphunzitsi yemweyo wachipembedzo amene anamutsutsa Yesu Khristu chifukwa cha zozizwitsa Zake ndi zizindikiro

ndi zodabwitsa, ndipo ankasiyana ndi Iye pa Lemba, anali wosabisa mokwana kubwera ndi kudzamuza Iye za izo. Mzimu womwewo ulipo mpaka mwa mphunzitsi wazampingo lero...?..okonzedweratu ndi Mulungu kuti akadze mpaka mu chiweruzo chimenecho. Ndicho chimene Baibulo linanena. “Amuna akale, okonzedweratu ku chiweruzo chimenechi, kuti asandutse chisomo cha Ambuye wathu chikhale chilakolako chonyansa.” Ndizo zolondola chimodzimodzi. Mu Yuda, ya 3—ndime ya 3 ya—ya Yuda, inu mukhoza kuzipeza izo. Ndiko kulondola.

<sup>123</sup> Zindikirani zinthu zonse izo kutsimikizira pamenepo, kuti chiripo chilemba cha chirombo. Apo ndi pamene izo ziri. Kotero pamene inu muzithamangathamanga pano kumanena, “Chabwino, ine ndidzasonyeza pamene chilemba cha chirombo chibwera,” khalani osamalira kuti musakhale muli nacho kale icho. Ndipo iwo amene ali nacho chotero, adzalangidwa mu moto ndi mwala wasulfure, kutsanuliridwira kwa chikho cha kuyipidwa kwa Mulungu, kuti akakhale ali kuzunzidwa usana ndi usiku, kwanthawi ndi kwanthawi. Ndi chinthu chowopsya. Tsopano kuthawa kwanu ndi kotani?

<sup>124</sup> Kukhala kuli nthawi, imene ikubwera pakali pano. Zindikirani, ndipo mu bungwe limenelo likusuntha... Tsopano ndiroleni ine ndikupatseni inu lingaliro pang’ono apa. Mu bungwe limenelo likusunthira mmusi monga choncho, ikubwera nthawi imene inu mudzayenera kukhala wa bungwe limenelo kapena inu simungakhoze kugula kapena kugulitsa; kapena kukhala ndi chilemba icho cha chinyenge, chilemba cha mpingo. Inu muyenera kukhala wa bungwe linalake kapena inu simungakhoze kugula kapena kugulitsa.

<sup>125</sup> Ndipo, mvetserani, kwa inu anthu amene mukudziwa chimene chiri Choonadi. Ine sindikunena kuti mukachoke ku mpingo wanu. Ine sindikunena kanthu kotsutsa wanu...za inu kapena za mamembala anu. Ine ndikunena za malikulu, kumbuyo kutali uko pamene iwo anapanga bungwe chinthucho, ndi kuchipanga icho, “Ife tizichita *izi*. Ife tizichita *izo*.” Ndipo iwo anakhazikitsa ulamuliro wa chibongachachitsulo. Ndipo Mulungu akuwugwetsa iwo mu zidutswa, ndi kuwutenga Mpingo Wake kutuluka mwa izo; nthawizonse ankachita zimenezo.

<sup>126</sup> Taonani mu ulendo wa ana a Israeli. Iwo anamanga moto. Iwo amakhalapo usiku uliwonse. Lawi la Moto limapachikika pamwamba pawo. Ndipo ine sindikusamala kaya ndi nthawi yanji ya tsiku kapena usiku imene iyo inali pamene Lawi la Moto ilo linkachoka, malipenga ankawombedwa ndipo Israeli ankanyamula msasa ndipo ankachokapo. Kaya uwo unali pakatipausiku, thuwu koloko madzulo, iliyonse imene inali, iwo ankanyamula msasa ndi kutsatira Lawi la Moto. Ndi kulondola

uko? [Osonkhana anena, “Ameni.”—Mkonzi.] Iwo ankatsatira Motowo.

<sup>127</sup> Chabwino, pamene Marteni Lutera anawona Moto wa Mulungu ukusunthira kunjja, Marteni Lutera anatuluka, kutsatira Moto kuchokera mu Chikatolika. Koma iye anamanga pansi pakepo ndipo anawupanga bungwe mpingo wake, ndipo iye sakanakhoza kusuntha.

<sup>128</sup> Motowo unasunthirabe kunjja, ndipo Wesile anawuwona Iwo, ndipo iye anapita mowutsatira Iwo. Ndiko kulondola. Moto wa Mulungu unamusiya Lutera atakhala. Ndiye, chinthu choyamba inu mukudziwa. Wesile anamanga pansi pa Iwo, mpingo wa Chiwesile wa Methodist.

<sup>129</sup> Ndiyeno panadza Alexander Campbell, John Smith ndi Chibaptisti, ndi zina zotero monga choncho, ndi Moody, ndi onse awo. Ndiye, chinthu choyamba inu mukudziwa, iwo anayamba kutenga mwambo, ndi kukhuthala, kuzizira, pamene aneneri akale anafa, ndi zina zotero. Gulu latsopano ili linabwera lopanda kanthu koma maphunziro a ku seminare, ndiyeno, chinthu choyamba inu mukudziwa, manja anafika mu mkate ndipo anawuwononga iwo.

<sup>130</sup> Ndipo Mzimu Woyera unasunthira kunjja, ndipo Achipentekoste anawuwona Iwo ndipo iwo anapita uko; kukhoza, unasuntha nawo, kutali kuchoka kwa Amethodisti ndi Abaptisti, ndi zina zotero. Tsopano chinthu chankhaza cha izo, koma kuti akwaniritse Mawu a Mulungu, Achipentekoste anapanga bungwe, ndi basi ozizira ndi amwambo monga ena onse a iwo. Koma, penyani, apo sipadzakhala konse m'badwo wina wa mpingo. M'badwo wotsiriza ndi M'badwo wa Mpingo wa Laodikaya, umene suli ngakhale wotentha kapena wozizira. Pafupi chipembedzo chokha chokwanira, pamene nyimbo ikuyimba, kuti avine chokwera-ndi-kutsika mu mipata, ndiyeno nkukhala pansi, kupita kunyumba ndi kukayankhula za woyandikana naye wanu.

<sup>131</sup> Chimene ife tikusowa lero ndi kachitidwe-kachikale, Mzimu Woyera, wotumizidwa ndi Mulungu, chitsitsimutso chimene chiti chidzakupangitse iwe kugona pa nkhope yako ndi kumalira, usana ndi usiku, ndi kulira ndi kususima, ndi kumapitiriza nazo, chifukwa cha machimo a dziko. Ife tifika mu zimenezo. Ndiko kulondola.

<sup>132</sup> Koma apo iwo ali. Basi ndi pamene ife tinafika, kufunda. Mulungu anati, “Basi zimangondidwalitsa Ine mmimba Mwanga! Ine ndidzangokulavulani inu muchoke mkamwa Mwanga.” Ndiwo mpingo, mpingo wa Protestanti, wokanidwa. Mpingo wa Protestanti uli wokanidwa; kuchokera kwa Pentekoste mpaka kwa Lutera, pang’ono paliponse pa Iwo. Mawu a Mulungu amanena choncho.

<sup>133</sup> Koma kuchokera mu uliwonse wa mipingo imeneyo, Iye watengamo Osankhidwa. Iye watengamo Mbewu kuchokera mwa umodzi uliwonse, kuchokera mu Methodisti, Baptisti, Presbateria, Luterani, onse kupyola kumeneko, Akatolika, ndi onse. Iye watengamo otsalira, kuwatengera anthu kunja.

<sup>134</sup> Kuno osati kale litali, dona wamng'ono atagona komwe kuno mu Louisville, Mkatolika, akufa. Ine ndinapita cha kumeneko. Ndipo wansembe anati, "Zamkhutu, kwa chinthu chotero!"

Ndipo mwamuna wake anati, "Khalani kumbali. Msiyeni iye abwere mkati."

<sup>135</sup> Ndinayenda kulowa mmenemo. Ndipo mkaziyo amayenera kuti akhale atafa mmawa wotsatira. Pamene ndinali kumupempherera iye, masomphenya anatulukira, ndipo anati, "PAKUTI ATERO AMBUYE." Ndiko kulondola. Mmawa wotsatira... Ndinamuuza iye maora angati amene izo ziti zidzakhale, chimodzimodzi basi mpaka ku dontho, pamene iye akanati adzapite kwawo wabwino. Iwo anaseka izo, monyodola. Ndipo ora lomwelo Mzimu Woyera unayankhula, iye anapita kwawo mkazi wabwino, ndipo ali bwino lero. Iye anali Mkatolika. Iwo anali Akatolika. Iwo *nkuti ali* Akatolika.

<sup>136</sup> Pamene iwe ulandira Kuwala... Mu Chipangano Chakale... Ndiroleni ine ndikuwonetseni inu chizindikiro chake tsopano. Mvetserani mwatcheru, ndiye ine ndipita molunjika ku phunziro langa. Penyani, mu Chipangano Chakale, pamene kapolo anali pansu pa ukapolo, ndiyeno iye anali naye... Iye anagulidwa kumeneko, ndi mtengo. Iye amayenera kumamutumikira mbuye ameneyo mpaka chaka cha chisangalalo. Ndipo pamene chaka cha chisangalalo chifika, apo panali lipenga limene linkawombedwa.

<sup>137</sup> Ndipo pamene kapolo anali kunja uko, iye ndi ana ake, ndi mkazi ndi onse a iwo akufuna kuti abwerere ku dziko la kwawo lakale. Iwo anali akupondaponda mu munda, ndipo wowagwiritsa ntchito akuwakwapula iwo, ndi njira *iyi* ndi njira *iyu*. Ndiyeno pamene wansembe wachisangalalo abwera, kuliwomba lipenga, ndipo wansembe uyo anakawomba lipenga, ndipo munthu uyo atalimva lipengalo. Iye akanakhoza kugwetsa khasu lake, iye akanakhoza kugwetsa chirichonse chimene iye anali akuchita, kuyang'ana mu nkhope ya womugwiritsa ntchito, ndi kunena, "Iwe sungakhoze kundimenya ine nthawi inanso kamodzi. Ine ndine mfulu." Kuchokapo kumene ndi kupita kwawo. Chifukwa chiyani? Apo pali kuomba kwa chisangalalo, pamene iwo amva kuwombako.

<sup>138</sup> Ndipo ndiwo Uthenga, chisangalalo, kuti iwe ndiwe mfulu kwa tchimo. Ndiwe mfulu kwa zizolowezi zonse zauve izi ndi zinthu zimene dziko labala pano mu dzina la chipembedzo, pansu pa zonse Chiprotestanti ndi Chikatolika, pansu pa chilemba cha chirombo. Ndiko kulondola. Ndiwe mfulu.



139 Iwe susowa kuti ukhale. Komano ngati munthu uyo akana kuti alandire icho, ndiye munthu ameneyo amatengedwa kuchokera pamenepo kupita pa mtengo wa guwa la mpingo, ndipo amayikidwa chilemba pa iye, kuboola bowo mu khutu lake. Ndipo iye anali wantchito kwa mbuye ameneyo malingana ngati iye anali moyo.

140 Ndipo inu mukukana kulandira Kuwala kwa Uthenga pamene Iwo ukulalikidwa mu Mphamvu ya Mzimu Woyera, mwa Baibulo, inu mukhoza kuzisindikizira nokha kopita kwanu Kwamuyaya. Amen.

141 Tsopano penyani, chinthu chimodzi chinanso chaching’ono, ngati inu mutandikhululukire ine chifukwa choyankhula chotero mphindi pang’ono zapitazo, za—za munthuyo. Koma, penyani pano, “Kunyenga Wosankhidwa amene. . .”

142 Tsopano, ife takhala tikuwagunda Achilutera, Abaptisti, ndi ena otero, ndi Akatolika, tsopano ndiroleni ine nditsikire kwa inu anthu achiyero miniti chabe. Mwaona? Ine ndimakhulupirira mu chiyero. Iwe uyenera kukhala woyera. “Popanda chiyero palibe munthu ati adzamuwone Mulungu.” Osati chiyero changa; chiyero Chake. Ndipo palibe kanthu kamene ine ndingakhoze kuchita za icho; ndicho chimene Iye wandichitira ine. Osati kuyima mu changa changa, chifukwa ine ndiribe chirichonse, sindiyesa nkomwe kuti ndikhale nacho chirichonse. Ine sindiyesa kuti—kuti ndikhale.

“Kodi inu mukuyesera kugwiritsitsa, M’bale Branham?”  
Ayi, bwana.

143 Ine ndimangolekerera, ndi kumulola Iye kuti agwiritsitse. Ndiko kulondola. Iye ndi Mmodzi Amene akugwiritsitsa. Kungokhala wakufa, ndicho chonse chimene iwe uyenera kuti uchite. Ingodzisungani nokha akufa, Iye adzagwiritsitsa. Iye wagwiritsitsa kale. Iye anagwiritsitsa pamenepo mpaka Iye anati, “Izo zatha.” Izo zinakhazikitsa icho. Mulungu akutilola ife kuchita icho, mofanana. Izo zatha.

144 Koma, anthu achiyero, inu Anazerini ndi a Pilgrim Holiness tsopano, kumbukirani. Pansi pa mphamvu ndi kutuluka kwa mpingo wa Chiwesile, kapena mpingo wa Methodist, pamene iwo anapanga bungwe, inu anthu okonedwa achiyero munatuluka, munati, “Ife tipitiriza chiyero.” Izo zinali zodabwitsa. Inu munangowusunga m’badwo umenewo, M’badwo wa Filadefiya uja, mpaka iwo utafika ku Laodikaya. Koma pamene ubatizo wa Mzimu Woyera unabwera, ndipo zizindikiro zitabwereranso ku mpingo, inu munazitcha izo “Mdierekezi.” Chifukwa iwo ankayankhula ndi malirime ndi kukhulupirira mu zinthu izi, inu munati, “Izo zinali za Mdierekezi.” Ndipo pamene inu munachita zimenezo, inu munachitira mwano Mzimu Woyera.

145 Ine ndinganene bwanji kwa dzanja langa, “Ine ndiribe chokusowera iwe”? Ngati pali aphunzitsi, pali kuyankhula mmalirime. Ngati pali alaliki, palinso mphatso ya machiritso. Phazi lingakhoze bwanji kunena kwa diso, “Ine ndiribe chokusowera iwe”? Mwaona? Iwe, ngati ndiwe mwana wobadwa wa Mulungu, iwe umayenda ndi kulandira chinthu chirichonse chimene Mulungu anena kuti ndi cholondola. Iwe umayenda kumene mu Kuwala.

146 Pamene iyo inali nthawi kuti Mpingo usunthe, Lutera anasuntha. Pamene iyo inafika nthawi kuti Mpingo usunthe dzanja Lake, Wesile anasuntha dzanja. Pamene iyo inafika nthawi kuti Mpingo uyankhule, Apentekoste inafika mpaka powonekera. Ndiko kulondola. Koma, tsopano, zindikirani.

147 Inu mukuti, “Nanga choyimira?” Inu mukuti, “Kodi chiripo choyimira cha izo?” Inde, bwana.

148 Kodi inu mukuzindikira kuti Yudasi Iskarioti, wotsutsakhristu weniweni, anali munthu wachipembedzo kwambiri? Kodi inu munali mutazindikira izo? Iwo anali nako kudalira kochuluka mwa iye, abale, mpaka iye anali msungichuma wa mpingo.

149 Ndipo Yudasi Iskarioti analungamitsidwa mwa chikhulupiriro, pokhulupirira pa Ambuye Yesu Khristu.

150 Iye anayeretsedwa kupyolera mu Mawu. Ahebri, 17:17... Ine ndikutanthauza, Yohane Woyera 17:17, “Ayeretseni iwo, Atate, kupyolera mu Choonadi; Mawu Anu ali Choonadi.” Ndipo Iye anali Mawu.

151 Ndipo iwo anapatsidwa mphamvu kuti apite kunja ndi kukalalikira Uthenga, ndi kukatulutsa ziwanda, ndi kukachiritisa odwala. Yudasi Iskarioti, Mateyu 10, anatchulidwa pakati pa iwo. Ndipo iwo anapita ndipo anakatulutsa ziwanda, ndipo analalikira Uthenga mwa njira yotero mpaka ochimwa analapa ndipo ziwanda zinachoka. Ndipo iwo anabwerera akusangalala ndi kufuula, ndi kukhala ndi nthawi yayikulu, monga msonkhano wawung’ono, wachiyero wa misasa. Ndipo Yudasi anali pomwepo ndi iwo. Ndizo zolondola chimodzimidzi, limodzi kumene ndi iwo.

152 Koma pamene inafika nthawi ya Pentekoste, Yudasi anawonetsa maanga ake.

153 Apo ndi pamene mpingo wachiyero unawonetsa maanga ake, pomwepo kumene, ndipo unapita kuseri kumene ndipo anaokana Mzimu Woyera womwe umene unali kuwatsogolera iwo ku Madzi akuya moposera; anazungulira kuseri ndipo anaokana iwo. Ine ndikudziwa kuti iwo anali nazo zochuluka za kutent-...

154 Ine sindine wa Pentekoste. Ine sindinakhale ndiri konse wa bungwe la Chipentekoste, ayi. Ine ndayima pakati pake.

Ine si wa Pentekoste, Methodisti, Baptisti. Ine ndine Mkhristu wa Baibulo basi. Ndizo zonse. Ine ndimakhulupirira chimene Mawu amanena. Ndipo ine sindingakhoze kukana mphatso ya kuyankhula mu malirime; ngati ine nditero, ine ndikana kuphunzitsa ndi mphatso ina iliyonse yowuziridwa. Ndiko kulondola. Ine sindinagwirizanepo nawo abale Achipentekoste pa “umboni wokha,” wa kuyankhula mu malirime. Ine sindimakhulupirira zimenezo. Tsopano, izo zonse nzabwino, ngati iwo amakhulupirira izo mwa njira imeneyo. Iyo ndi ntchito yawo, onani, koma ndizo mwangwiro bwinobwino. Ine . . . Paulo anati, “Ine ndikanakonda kuti inu nonse muziyankhula ndi malirime.” Ine ndikanakonda kumuwona aliyense kukhala pafupi chotero kwa Mulungu.

<sup>155</sup> Iwo ali nazo zochuluka za kudzipangitsa, zochuluka za chikhulupiriro chabodza. Iwo ali nazo kunjira uko, nthawi zochuluka, ndipo ankachita ngati kuti iwo anali ndi Mzimu Woyera, ndipo ankanena chinachake chimene sichinali kuyankhula mumalirime. Moyo wawo unkatsimikizira chimene icho chinali. Koma pakhala pali nkhani yowona yeniyeni ikuchitikabe mofanana basi, nthawi yonseyo.

<sup>156</sup> Chabwino, nchifukwa chiyani Mdierekezi sanati aponyere uko nyambo ya khwangwala wapachibwanawe? Zedi, iye angatero, kuti ayesere kulepheretsa. Iye anaponyera uko chinthu chomwecho mu chiyero. Iye anaponyera uko chinthu chomwecho mu Methodisti. Iye anaponyera uko chinthu chomwecho mu tsiku la Lutera. Ndipo iye akuponyera chinthu chomwecho lero. Ndipo pansa pa mphamvu ya mphatso, za machiritso Auzimu, ndi kudziwa za mmitima, iye akuponyera zinthu zomwezo kunjako.

<sup>157</sup> Koma kodi chowopsyezera khwangwala chimatanthauza chiyani kwa inu, ngati inu mukanati muziyankhula mayankhulidwe a mbalame? Mbalame nkuti, “Pamene ine ndiwona chowopsyezera khwangwala, ndicho chiphaso cha zakudya. Ma aapulo abwino amene alipo, ali pozungulira kumene ndodo zonsezo zagona ndipo zowopsyezera akhwangwala zachita kupachikidwapo.” Ndiko kulondola.

<sup>158</sup> Koma inu mukuona momwe mzimu uwo unasanthira kumene kuno. Ndipo Yesu anayang’ana ndipo anawoneratu izo kupyolera mu mpingo wa Katolika uwo, ukutuluka. Anati, “Musati mumutche munthu aliyense bambo. Musati muzigwiritsa ntchito obwereza mwachabe, zinthu zonse izi.” Anatuluka uko ndipo anati, “Tsopano khalani osamala kwambiri, wotsutsakhristu adzakhala wapafupi kwambiri mpaka iye adzanyenga Osankhidwa amene ngati nkotheke.”

<sup>159</sup> Penyani, m’bale, ndi anamwali angati anapita kuti akakomane naye Ambuye? Khumi. Onse a iwo anali anamwali. Kodi *chiyero* chimatanthauza chiyani? “Wangwiro, woyera,

namwali.” Khumi a iwo anali anamwali. Asanu analibe Mafuta mu nyali zawo. Asanu anali ndi Mafuta mu nyali zawo. Asanu *awa* anali basi oyera chimodzimidzi ndi anamwali monga *awa* anali. Koma kodi *Mafuta* amayimira chiyani, mu Baibulo, kumene ife tinatengako izo usiku watha, usiku wadzana? Mzimu, “Mzimu Woyera.” Iwo anadziyeretsa okha ndi kukhala pamenepo, koma iwo anali amantha ndipo anayima kutali ndi Kasupe amene anatsanulira mu Mafuta. Mwaona, anadzipanga bungwe okha ndipo anakhazikika pansi, ndipo pamenepo iwo ali, ofunda. Ndiko kumene m’badwo wa mpingo unapita.

<sup>160</sup> Tsopano, tsopano ife tikubwera ku chilemba cha Mulungu. Ine ndiri ndi maminiti makumi atatu, Ambuye akalola. Tsopano ine ndikufuna inu mutembenuze ndi ine, choyamba, ndi kupeza kufunika kwake, chilemba ichi cha Mulungu.

<sup>161</sup> Kumbukirani chimene chilemba cha chirombo chiri; osati chikominisi. Chilemba cha chirombo chimachokera ku Roma, mu dziko lonse; Chikatolika, ndi Chiprotestanti chinalumikizana mwa icho, chipembedzo chabungwe. Ndipo iwo agwirizanitsitsa mipingo mpaka mpingo uliwonse udzayenera kuti ugwadire kwa chinthu chimenecho, ochokera mzipembedzo zathu akankhidwira pa mzere wa kumbali. Ndiko kulondola.

<sup>162</sup> Chivumbulutso mutu wa 9 tsopano. Tiyeni tiwerenge mwatcheru kwenikweni pano kwa mphindi zingapo, ngati Mulungu alola, ndi kuwona chimene Iye ananena mu Mawu Ake. Tsopano . . . [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] . . . wa—wa Chivumbulutso, ndipo ndime ya 4. Mvetserani kwa izi.

*Ndipo icho chinalumuliridwira iwo (pamene iwo awona miliri ili kutsanuliridwa) kuti iwo asawononge udzu kapena mitengo . . . ngakhale chinthu chobiriwira chirichonse, ngakhale mtengo uliwonse; koma . . . anthu awo amene alibe chisindikizo cha Mulungu mu mphumi zawo.*

<sup>163</sup> Pamene miliri inali kubwera, chinthu chokha chinali chotetezedwa chinali iwo amene anali atasindikizidwira kutali mu Ufumu wa Mulungu. Uku ndi kufufuza chiweruzo, pamene anthu . . . Ndipo ngati Mulungu ati andithandize ine, mu maminiti angapo inu muziwona izo mwa Mawu a Ambuye, kuti iyi ndi nthawi ya kusindikiza kwa malo. Ndipo iwo amene akukana Iko, palibe kanthu kati katsalire koma chiweruzo Chamuyaya.

<sup>164</sup> Tsopano ife tipita mpaka mu Chipangano Chakale. Ndipo tiyeni tipite cha apa, ngati inu mungafune, ku Bukhu la Ezekieli, ngati inu mungafune, ndipo tiyeni tiwerenge kwa kanthawi mu Ezekieli 9. Tsopano, mwa kuthandiza kwa Mulungu tsopano, Iye atatithandiza ife. Ndi kukhazikitsa pansi tsopano mwa kuphunzitsa, kwa maminiti makumi atatu otsatira

okhawa, ngati Mulungu alola. Tsopano izi ndi zokhudzana, inu mukulemba izo, Ezekieli 9, izi ndi zokhudza . . .

165 Chinthu choyamba chimene ife tiyenera kuti tikhale titachikhazikitsa tsopano, kodi Chisindikizo cha Mulungu ndi chiyani? [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] Kodi inu simukuganiza kuti izo zingakhale zofunikira? [Osonkhana, “Ameni.”] Kodi Baibulo ndi Mawu abwino mokwanira kwa inu? [“Ameni.”] Tsopano ine ndikudziwa kuti inu muli nazo izo, iwo amene amati, “Kusunga tsiku la sabata,” koma palibe chidutswa chimodzi cha Lemba lothandizira zimenezo, mu Chipangano Chatsopano. Tiyeni tipeze chimene Chisindikizo cha Mulungu chiri, zoonadi. Tembenuzani ku Aefeso 4:30, 4:30, ndi 1:13. Lembani izo pamenepo. Aefeso 4:30 amati:

. . . *musati mukwiyitse Mzimu woyera wa Mulungu, umene inu muli osindikizidwa nawo mpaka tsiku la chiwombolo chanu.*

166 Tsopano, kodi *kusindikiza* kumatanthauza chiyani? Kusindikiza ndi “chizindikiro cha kutsiriza.” Ndi kulondola uko?

167 Chabwino, kodi inu munayamba mwawona choyendapanjanji chikukweza magalimoto? Iye amatuluka panja ndi kukhala mochuluka chotere *apa*, ndi mochuluka chotere *apa*. Woyang’anira amabwera pamenepo, iye amayang’ana mkati; ndipo ngati *iyi* ili yomasuka pang’ono, ikugwadera, “Ayi. Ine sindiyisindikiza iyo. Muyenera kuying’amba iyo ndi kuchitanso izo kachiwiri.” Chinthu chotsatira, iye ayesa kulongeza izo kachiwiri; iye apeza izi molakwika. Woyang’anira abwera pamenepo, “Mwalakwitsa. Chitaninso izo kachiwiri.”

168 Ndipo ndicho chimene Mulungu wakhala akuchita ndi mpingo Wake kwa nthawi yaitali. Inu mukalondeza, ndipo inu mukupita Kumwamba; inu mukatenga chirichonse ndi inu. Masewero anu a juga, nhu, chinthu china chirichonse chimene inu mukanakhoza kulongeza mu mpingo, inu mukayesa kuti muchitenge icho ndi inu. Mulungu amangotsutsa izo; simuli okonzeka kuti musindikizidwe.

169 Koma pamene Mulungu amuwona munthu, wokhudzidwa, mzimu wosweka, woona mu mtima, pansi pa guwa apo, Mulungu amatseka chitseko cha dziko kwa iye, ndi kumusindikiza iye mkati mmenemo ndi ubatizo wa Mzimu Woyera, ndipo izo zimakhlapo mpaka Yesu atabwera; osati kuchokera ku chitsitsimutso chimodzi kumka ku chimzake, koma, “mpaka tsiku la chiwombolo chanu.”

170 Pamene bokosi la galimoto, chitseko, chikatsekedwa, ndipo chisindikizo cha boma chitayikidwa pa icho, icho sichingakhoze kutsegulidwanso mpaka iyo itakafika kopita kwake kotsirizira.

<sup>171</sup> Ndipo munthu aliyense yemwe wabadwa kachiwiri ndipo atasindikizidwira kulowa mu Ufumu wa Mulungu, alibenso chikhumbo cha dziko mpaka tsiku limene Yesu Khristu amutengere iye kulowa mu Ufumu. Kotero ngati inu mukukhala ndi vuto, ndi kumanena kuti inu muli nawo Mzimu Woyera; kaya ndinu wa mpingo wa Methodisti, mpingo wa Baptisti, mpingo wa Pentekoste; kaya inu munafuula, munayankhula ndi malirime; kubatiza chamtsogolo, chambuyo, kukonkha; ngati inu mukukhalabe ndi mavuto a mtundu umenewo, inu kulibwino mubwerere ndi kudzafufuza pa katunduyo. Ndiko kulondola. Mwatenga zochuluka limodzi nanu; izo zamasuka kwambiri, zikugwedezeka. Mulungu samasindikiza izo mwa njira imeneyo.

<sup>172</sup> Pamene njere ya tirigu igwera mu nthaka, ziribe kanthu. . . Ngati njere ya tirigu iyo ifa kwa iyoyokha, iyo siyingakhoze kubala chisoso, kuti ipulumutse moyo wake. Njere ya tirigu idzabala njere ya tirigu, basi motsimikiza monga chirichonse. Ndipo ngati ife tafesedwa ndi Mbewu yosavunda ya Mulungu, Iyo ingakhoze bwanji kubala chirichonse koma moyo wa Moyo wa Khristu?

<sup>173</sup> Mzimu Woyera ukutsogolera Mpingo, kuwutsogolera Iwo mu Mphamvu ya chiwukitsiro cha Yesu Khristu, ndipo inu mwasindikizidwa mpaka tsiku la chiwombolo. Ndilo Baibulo. “Musati mukwiyitse Mzimu Woyera wa Mulungu, umene inu mwasindikizidwa nawo mpaka tsiku la chiwombolo chanu.” Aefeso 4:30.

<sup>174</sup> Tsopano, Mzimu Woyera usanabwere nkomwe, iye wasindikizidwira kutali m’badwo wa Amitundu usanayambe nkomwe. Iye wasindikizidwira kutali pansu pa zoyikapo nyali za golide izo, (ife tinali nacho chojambula, kuti timvetse izo), kumbuyo uko pansu pa m’badwo umenewo.

<sup>175</sup> Iye anali akupusitsana nawo iwo uko kupyola mwa Abrahamu, Isaki, Yakobo, Davide, ndi onse uko kupyola mu m’badwo wa mdima umene iwo anali nawo mu masiku a Ahabu, mpaka pansu, Solomoni, ena otero, mpaka izo zitafika mu chikhalidwe chofunda chija. Koma basi Iye asanati atseke nyengo imene ija kumeneko, Iye anapereka ukoma wawukulu wa Mzimu Woyera kwa Ayuda okha, “Musati mupite mu njira ya Amitundu, koma mupite kwa nkhusa zotayika za Israeli.” Kodi nkulondola uko? “Iye anadza kwa Ake omwe, ndipo Ake omwe sanamulandire Iye ayi.”

<sup>176</sup> “Koma onse amene anamulandira Iye, anawapatsa Iye Mphamvu kuti akhale mphukira za Mulungu.” Iye anati, “Ine ndikupereka kwa iwo Moyo Wamuyaya.” *Moyo Wamuyaya umachokera ku mawu Achigriki “Zoe.” Zoe ndi Moyo umenewo. Zoe ndi Moyo wa Mulungu. Ndipo ngati Moyo wa Mulungu ukhala mwa inu, ubala moyo waumulungu basi motsimikiza monga ine ndikuyima mu nsanja iyi. Ndipo munthu yemwe ali*

nawo Iwo, sangakhoze kutayikanso kuposa momwe Mulungu sangakhoze kutayika, chifukwa Mulungu ali mwa munthuyo. Ameni. “Iye amene amva Mawu Anga, ndi kukhulupirira pa Iye amene anandituma Ine, ali nawo Moyo wosatha, ndipo sadzafika ku chiweruzo; koma ali nawo Moyo wosatha.” “Iye amene adya thupi Langa ndi kumwa Magazi Anga, Ine ndidzamuukitsa iye mu tsiku lotsiriza.” Ndiwo Mawu Ake. Ndi chitonthozo chotani kwa wokhulupirira! Ndipo ndi chiweruzo chotani kwa iwo amene akukana kuti ayende mu Kuwala.

<sup>177</sup> Kukuyamba kufunda, si choncho? Chabwino, Ndi zabwino kwa inu. Zindikirani, onani ngati izi ziri zoon. M’bale, ife tikhoza kutenga izo, Lemba pambuyo pa Lemba, sabata pambuyo pa sabata, sabata pambuyo pa sabata, ndi kukhala pa izo, mpakana...phunziro lomwelo, kwa chaka, komabe osalikoka ilo kuchokera mu Baibulo, zonse za izo, ndipo pa chinthu chomwecho kumene.

<sup>178</sup> Tsopano mwa kuyambirira kochepe chabe apa, ife tikupita kumbuyo ndi kukapeza chimene kukana ubatizo wa Mzimu Woyera chimatanthauza kwa inu, chimene icho chinatanthauza kwa iwo mu tsikulo.

<sup>179</sup> Tsopano, mu Ezekieli mutu wa 9, mneneri anawona Yerusalemu. Tsopano kumbukirani, ife tikuyankhula za mu kadanga kameneko uko, Ayuda, kusanafike kumene kutsirizika kwawo.

<sup>180</sup> Tsopano ife tiri mwa Amitundu, pa kutsirizika kwawo. Ndiye ife tikupita mpaka mu Zakachikwi. Chabwino.

<sup>181</sup> Koma tsopano penyani, inu mukuthana nawo Ayuda tsopano. Mneneri akuwoneratu izo. Izi ndi zaka zana apabe, pafupi mazana asanu ndi atatu, kusanafike kudza kwa Ambuye, ndipo izo zinaloseredwa ndi mneneri. Tsopano mvetserani mwatcheru pamene ife tikuwerenga.

*Iye anafuulira aponso mu makutu anga ndi liwu lokweza, kunena, Apangitse iwo amene ali nako kuyang’anira pa mzinda kuti asendezere pafupi, ndipo munthu aliyense ali ndi chida chophera, kapena chida chowonongera mu dzanja lake.*

<sup>182</sup> Tsopano penyani mwatcheru tsopano pamene ife tikuwerenga.

*Ndipo, taonani, amuna asanu ndi mmodzi anabwera kuchokera ku...chipata chapamwamba, chimene chiri cha kumpoto, ndipo munthu aliyense ali ndi chida chophera mu dzanja lake; ndipo mwamuna pakati pa iwo, ali ndi zovala zoyera, atavekedwa mu bafuta, ali ndi nyanga ya inki ya wolemba cha pambali pake: ndipo iwo anapita...ndipo anakaima patsogolo, pambali pa guwa lamkuwa.*

*Ndipo ulemerero wa Ambuye Mulungu wa Israeli unapita mmwamba kuchokera kwa mkerubi, pamene iye anali, mpaka ku chiunda cha nyumba. Ndipo iye anayitana kwa mwamuna wovekedwa mu bafuta, yemwe anali ndi nyangayainki ya olembera cha pambali pake; (mvetserani)*

*Ndipo AMBUYE ananena kwa iye, Pita pakati pa mzinda, kupyola pakati pa Yerusalemu, (kokafika nku Yerusalemu), ndi kukayika chilemba pa mphumi ya anthu amene akuusa moyo ndi...kulira chifukwa cha...zonyansa...zochitidwa pakati pake.*

*Ndiyeno kwa enawo iye anati mu khutu langa, Pitani...atsatireni iwo kupyola mu mzinda, ndi kuwakantha: ndipo musati mulole diso lanu lilekerere, ngakhale kukhala nacho...chisoni:*

*Mukaphe psyiti nkhalamba ndi aang'ono, adzakazi onse...ana aang'ono, ndi akazi: koma musati muyandikire kwa aliyense pa yemwe...chilemba; ndipo iye anayambira ku malo opatulika. Ndipo... kuyambira kwa nkhalamba za amuna zimene zinali pakhomo pa nyumba.*

<sup>183</sup> Tsopano penyani mneneri mu Mzimu, kutengedwera mmwamba mu Ulemerero. Mulungu anati, “Ine ndikusonyeza iwe momwe ine nditi ndikhazikitsire izo ndi Ayuda, ndisanabwere kwa Amitundu.” Werengani ndime, kapena mutu usanafike uwu. Tsopano, pamene iye anabwera mmenemo, iye anati, “Ine ndinawona...” Poyamba, iye anawona tchimo mu mzinda, monga iye anali asanaliwonepo kale, ndipo iye anawona Yerusalemu. Tsopano kumbukirani, izo zinali zokafikira kwa Ayuda okha, osati Amitundu; Myuda, ndi likulu lawo, Yerusalemu. Monga ngati usiku watha, ife tinali nazo izo zokafikira kwa Achiprotectanti; tsopano, usikuuno, ndizo kwa Myuda. Iye anati, “Pitani kupyola mu mzinda.” Apa pakubwera amuna ali ndi zida zophera mmanja mwawo, akupita patsogolo kukapha chirichonse mu mzinda. Iye anati, “Tsopano ingogwirani izo, miniti chabe.”

<sup>184</sup> Ndipo kuchokera kumeneko kunadza Mwamuna wovekedwa mu zoyera. Tiyeni tiyime kaminiti. “Wovekedwa mu zoyera,” chilungamo, chiyero. “Wovekedwa mu zoyera,” Yemwe anali ndi nyangayainki pa mbali Yake. Iye anati, “Pita kupyola mu mzinda poyamba, iwo asanabwere, ndipo kayike chilemba pa mphumi, chilemba pa mphumi ya mwamuna aliyense, mkazi, mnyamata, ndi msungwana, mu mzinda, amene akuusamoyo ndi kulira chifukwa cha chonyansa chomwe chachitidwa mu mzinda, chifukwa cha machimo a anthu.” Kayikeni chilemba pa iwo!

<sup>185</sup> Ndiyeno, Iye atatha kupyolamo ndi kuyika chilemba, Iye anabwerera mmbuyo ndipo anati, “Izo zachitika.”



186 Ndiye Iye anatumiza amuna, anati, “Pitani uko, ndipo musati mukalekerere kanthu, koma inu mukaphe psyiti chirichonse chimene chiribe chilemba chimenecho pa icho.”

187 Penyani kuno, m’bale. Woyika Chilemba uyo sanali wina kuposa Mzimu Woyera.

188 Ndipo zindikirani, ngati Iye atabwera ku Jeffersonville, usikuuno, ku Branham Tabernacle, kapena kachisi wina aliyense mu mzinda, kapena mpingo wina uliwonse, kodi Iye angayike chilembacho pa ndani, yemwe anali wodzipereka kwambiri ndi woona mtima pamaso pa Mulungu mwakuti amalirira ndi kufuulira, ndi kupemphera usana ndi usiku, chifukwa cha tchimo la mzinda? [M’bale Branham agogoda pa guwa kawiri—Mkonzi.]

189 Kodi Ichu chingachite chiyani kwa alaliki amene amawalola akazi awo kutuluka kunja kuno mu zovala zosambira, ndi kudziwongola mu akabudula, ndi kumayenda chokwera-ndi-chotsika mmisewu; ndi kumakayimba mu kwayara, ndi kudzipaka utoto ndi kumachita ngati Mayezebeli. Ndipo pamene... Amuna kunja uko, akusuta, ndi kumwa, ndi kumapitiriza, ndi kuchita juga, ndi china chirichonse! Ndipo iwo amachita ngati kuti iwo anali osakhudzidwa za izo; kumapita ku chakudya chachikulu china cha nkuku, kapena phwando kwina wake. Kutsala ku nyumba Lachitatu usiku ndi kumayang’ana pa televizioni, mmalo mwa kukakhala nawo pa msonkhano wa pemphero. Mu nthawi ya chirimwe, kutseka tchalitchi, kwa misonkhano. Iye akanati asindikize chiyani?

190 Chimene ife tikusowa, usikuuno, ndi zochuluka za izi kuno za kulalikira kwa ku Hollywood kotsamwitsidwa! Ndi chitsitsimutso cha kachitidwe kachikale, chotumizidwa ndi Mulungu, amuna ndi akazi amene amafika pa guwa! Ndi kusiya zogwedezana chanza izi, ndi kumagwirana manja, ndi kuwakonkha iwo, ndi kumabatiza nkhope chamtsogolo, Chambuyo, ndi zonse zina izi za mawonekedwe aang’ono ndi timalingaliro. Ndi kufika mpaka ku chenicheni, kukhudzidwa, mzimu wosweka, pamene tchimo liripo. Sakanizani izo palimodzi, ndi kuyamba kulirira kwa kachitidwe-kachikale, kwa mwana wobadwa-mwatsopano. Amen. Ndiwo mtundu umene umalandira Mzimu Woyera. Ndiko kulondola.

191 Ziribe kanthu kaya iwo ndi Amethodisti, Abaptisti, kapena Akatolika, kapena chirichonse chimene iwo ali! Pamene iwo afika patsogolo pa guwa limenelo ndi kulira, usana ndi usiku, “O Ambuye Mulungu, yang’anani pa machimo a mzinda uwu! Mtima wanga sungakhoze kupuma! Ine sindingakhoze kupuma, Ambuye, kuti ndiwone zinthu izi zikumapitirira. O Mulungu, chitani chinachake! Titumizireni ife chitsitsimutso cha kachitidwe-kachikale,” muli pa mzere wammalire wa kulandirira Mzimu Woyera ndiye, m’bale! . . . ? . . .

<sup>192</sup> Koma ngati inu muyenda pamwamba apo chifukwa chakuti munalumphapo mmwamba-ndi-pansi, kapena chifukwa inu munavina nayo nyimbo, kapena chifukwa inu munachita chinthu chinachake; ndipo mumayenda pozungulira ndi kumafufuma, ndi wosakhudzidwa, ndi kulalata, ndi kumakangana, ndi kujowina-mpingo, ndi kumalumphaka kuchokera pa malo kupita ku malo; izo zikusonyeza inu munali musanapeze konse kanthu mu chiyambi.

<sup>193</sup> M'bale, amenewo, ndiwo mankhwala abwino amphamvu, koma iwo ndithudi akukonzani inu. Ndiko kulondola. Inde, bwana. Iwo akutengerani inu kunja, popanda wofooka mmodzi pakati panu.

<sup>194</sup> Monga Mose. Ine ndikufuna kuyang'ana mu bokosi lake la mankhwala, mungafune inu? Anali nawo anthu mamilioni awiri kumeneko. Kodi inu mungafune kuyang'ana mu bokosi la mankhwala la Mose, chimene iye anali nacho? Amuna onse okalamba awo, ndi mazana a ana aang'ono obadwa usiku uliwonse, ndi anthu olumala, ndi anthu odwala. Ndipo pamene iye anatuluka, mu zaka makumi anai, uko kunalibe ngakhale mmodzi—mmodzi wofooka wina pakati pawo. Kodi simukanafuna ena a inu madokotala, amene mwakhala pano usikuuno, kufuna kuti muwone mu bokosi lake la mankhwala?

<sup>195</sup> Tiyeni tiyang'ane mwa ilo ndipo tiwone chimene ilo liri. Tsopano penyani kumbuyo. Ife tipeza izo. “Ine ndine Ambuye amene amakuchizani inu.” Ndi zimenezo. “Ameni.” Ndicho chimene iwo anali. “Ine ndine Ambuye amene amakuchizani inu.” Kuti pakhala mwana yemwe ati abadwe. “Ine ndine Ambuye amene amakuchizani inu.” Iye ali ndi chibayo. “Ine ndine Ambuye amene amakuchizani inu.” Ndilo dongosolo lokhalo limene iye akanakhoza kupereka. Ndi lokhalo limene iye ankalisowa. Ndi lokhalo limene iye anali nalo. Ndicho chimene Mulungu anapereka kwa iye.

Ndithudi, lero, “O, ife sitimakhulupirira mu Zimenezo. Ayi, izo. . .”

<sup>196</sup> Mulungu samasintha konse. Iye ali chimodzimodzi. Ngati mzimu uwu, umene ukumapitiriza mwa njira imene anthu amachitira lero, pansu pa dzina la Chikristu, unamupangitsa Mulungu kudwala mmimba Mwake mmbuyo umo, chinali “chonyansa” kuti anthu achite izo, ndi chonyansa lero. “Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse.” O, ine ndikumverera mwachipembedzo.

<sup>197</sup> Zindikirani, “Pitani apa,” Iye anati, “Inu mupite kupyola mu mzinda ndipo Inu mukayike chilemba pa iwo amene akuusa moyo ndi kulira chifukwa cha chonyansa chimene chikuchitidwa mu mzinda.” Ndiyeno Iye anati, “Inu mutatha kuchita izo,” Iye anawatembenuza anthu awa okhala ndi zida zophera patsogolo, ndipo iwo anapita uko ndipo anapha chirichonse.

198 Tsopano, wazambiriyakale, mphindi chabe. Yesu anadza mu thupi; Mulungu, anawonekera mu thupi. “Mulungu anali mwa Khristu, akuliyanjantsa dziko kwa Iyemwini.” Ndipo pamene Iye anadza mu thupi, Iye anapita mozungulira akuphunzitsa. Iwo anamutcha Iye “Belezebule,” wam’bwebwe. Iwo anamuseka Iye, za mabadwide Ake, china chirichonse; anamukana Iye, anamutayira Iye kunjja.

199 Iye anati, “Aliyense yemwe ayankhula motsutsa Mwana wa munthu, izo zidzakhululukidwa kwa iye, koma aliyense amene ayankhula motsutsa Mzimu Woyera, izo sizidzakhululukidwa kwa iye, mu dziko ili ngakhale dziko likudzalo.”

200 Iye anawayitana Ayuda ochepa palimodzi. Iye sanapite kwa Amitundu. Iye anapita kwa Ayuda. Iye anatumidwa kwa Ayuda; iyo siyinali nyengo ya Amitundu. Muni wotsiriza unali ukuyaka mu m’badwo wa Chiyuda, ndipo Iye anapita kumeneko. Ndipo uko kunali anthu pang’ono amene anamulandira Iye, oyitanidwira kunjja.

201 Chimodzimidzi basi monga izo ziriri lero. Basi monga Mzimu Woyera ukuyankhula kuchokera mwa Yesu Khristu, unayitana panthawiyo; kotero uli Mzimu Woyera kuyankhula kuchokera mwa Yesu Khristu, ukuitanira kunjja, lero.

202 Iwo ankakhulupirira zauzimu. Iwo ankamupenya Mtsogoleri wao. Iwo anamupenya Iye. Iwo ankadziwa kuti Iye anali mfumu ya aneneri. Iwo ankadziwa chirichonse chimene Iye anali. Chimene Iye ankayankhula, Mulungu ankachitsimikizira icho ndipo ankati icho chinali Choonadi. Iwo ankadziwa kuti iwo anali nacho Choonadi. Iwo ankadziwa Yemwe iwo anali kumukhulupirira, ndipo iwo anapitirira patsogolo ndi Yesu.

203 Ndiye iwo anamupachika Iye. Iye anati, “Atate, akhululukireni iwo, iwo sakudziwa nkomwe chimene iwo akuchita.”

204 Koma pamene Tsiku la Pentekoste linadza mwathunthu, apo panali gulu laling’ono, la anthu olira, akulira ndi kumapitiriza. “Ndipo pamene Tsiku la Pentekoste linadza mwathunthu . . .”

205 Mwadzidzidzi apo panadza wansembe uko mu msewu, ali ndi bokosi la tokulumunya, bokosi la mgonero, anati, “Sololerani kunjja lirime lanu tsopano, ndipo ine ndimwa vinyo”? Ndi zamkhutu bwanji! Akukwera msewu anadza mlaliki wa Pentekoste, ndipo anati, “Ife titenga dzanja lamanja la chiyanjano, ndi kutenga miyezi isanu ndi umodzi ya kuletsedwa”? Ha! Zamkhutu! “Ine ndikukonkhani inu. Ine ndikubatizani inu. Ine ndikutengerani inu njira *iyi*, kukutengerani inu mu mpingo, kukupatsani dzanja lamanja la chiyanjano”? Zamkhutu!

206 “Koma pamene Tsiku la Pentekoste linadza mwathunthu, mwadzidzidzi apo panadza kuchokera Kumwamba mkokomo wa mphepo yaikulu, ndipo Iyo inadza nyumba yonse momwe

iwo anali atakhalamo. Malirime amoto anakhala pa iwo, ngati moto.” Iwo anayamba chibwibwi, ndi kudodoma, ndi dovu, ndi malovu, ndi kumapitiriza.

207 Inu mukuti, “Ayi!” Ine nditsimikizira izo kwa inu ndi Baibulo. Inde, bwana. “Inu mukutanthauza kuti mundiuze ine ndicho chimene iwo anachita?” Ndicho chimene Baibulo linanena.

208 Kodi inu mumadziwa kuti Yesaya analosera? Ndiroleni ine ndikuwerengereni inu chinachake chaching’ono kuchokera mu Yesaya pano, miniti chabe. Yesaya, mutu wa 28, ndipo kuyambira ndi ndime ya 8.

*Pakuti magome onse adzazidwa ndi masanzi... (akuyankhula za tsiku lino)... ndi uwe, kotero kuti palibe malo oyera. (M’bale, ngati icho sichinali chithunzi cha Myuda!)*

*Kodi iye adzaphunzitsa ndani chidziwitso? ndipo ndani yemwe iye ati adzamupange kumvetsa chiphunzitso? (ife tikuyankhula za Chiphunzitso, usikuuno)... iwo amene aletsedwa kuyamwa mkaka, ndi iwo amene achotsedwa pa mabere?*

*Pakuti langizo liyenera kukhala pa langizo, langizo pa langizo; mzere pa mzere, mzere pa mzere;... (umo ndi momwe Uthenga umadzera, kuchokera ku Genesis mpaka ku Chivumbulutso!)*

*Pakuti ndi milomo yachibwibwi ndipo ndi lirime lina Ine ndidzayankhula kwa anthu awa.*

*... ndipo uwo ndiwo mpumulo, mtendere umene ine ndinanena kuti uyenera kubwera. Ndipo pakuti zonse izi sadzazimvetsa, koma anachokapo, akugwedeza mitu yawo.*

209 Pamenepo inu muli. Ndicho chimene Iye ananena. Awo sanali mawu anga; awo ndi Mawu Ake. Sankhani inu, ngati inu mungakhoze. Iwo sangakhoze konse kusinthidwa. Iye anati, “Langizo pa langizo; mzere pa mzere; kuno pang’ono ndi uko pang’ono.” Uthenga wonse uyenera kubweretsedwa panja.

210 Uthenga wathunthu uyenera kuyambira kuno, ndipo iwo anawulalikira Iwo. Ndipo pamene iwo anatero, Mphamvu ya Mzimu Woyera inadza.

211 Ndipo Ayuda amenewo anali atamuseka Yesu, koma iwo anaseka, anati, “Ha-ha-ha! Anthu awa aledzera vinyo watsopano.” Iwo anasindikiza kopita kwawo Kwamuyaya. Iwo anati, “Nchifukwa chiyani kuti ife tikukhoza kuwamva mu lirime lathu lomwe, ntchito zodabwitsa zimene iwo akuyankhula? Bwanji, anthu awa aledzera vinyo watsopano. Ha-ha!” Iwo anawanyoza ndi kuwaseka.

<sup>212</sup> Ndipo Petro, woyera-wodzigudubuza wamng'ono uja, mlaliki wa pa bokosi la sopo, atamuyikira iye kunja pa bokosi la sopo, ndi kudumphira pa ilo. Anati, "Inu amuna a Yudea, ndi inu amene mumakhala mu Yerusalemu, mulole ichi chidziwike kwa inu, ndipo mvetserani ku liwu langa. Koma ichi chiri—ichi ndi chija chinanenedwa ndi mneneri Yoweli. Anthu awa sanaledzere vinyo watsopano, monga inu mukulingalira, pakuti ndi ora lachitatu la tsiku. Koma ichi ndi Chija." Iye anawalozera mmbuyo ku Baibulo. Ine mowirikiza ndati, "Ngati ichi si Chija, ine ndingochisunga ichi mpaka Icho chitadza, ngati pali kusi yana kulikonse." Kulondola. Anati, "Ichi ndi chija chimene chinayankhulidwa ndi mneneri Yoweli. Icho chidzachitidwa mu masiku otsiriza," zaka zikwi-ziwiri zotsiriza.

<sup>213</sup> Zikwi-ziwiri zoyamba, analiwononga dziko ndi madzi. Zikwi-ziwiri zachiwiri, Khristu anadza. Mu zaka zikwi-ziwiri zotsiriza, "Ine ndidzatsanulira Mzimu Wanga." Aleluya! Osati "Ine ndidzaphunzitsa alaliki ena ndi kutumiza ansembe ena."

<sup>214</sup> "Koma ine ndidzatsanulira Mzimu Wanga kuchokera Kumwamba uko; ana anu aamuna ndi aakazi adzanenera; pa adzakazi Anga aamuna ndi adzakazi achikazi Ine ndidzatsanulirapo za Mzimu Wanga, ndipo iwo adzanenera. Ine ndidzasonyeza zizindikiro mu miyamba kumwamba, ndi mu dziko lapansi pansi." Ndicho chimene icho chinali. Uko kunali kutsegulira.

<sup>215</sup> Ndipo Ayuda amenewo anaseka ndipo ananyodola, ndipo anati, "Iwo akhuta vinyo watsopano." Izo zinasindikiza kopita kwawo.

<sup>216</sup> Mu a.d. 96, kubwera kwa Tito, akubwera pansi kuchokera ku chigawo, Yerusalemu anazingidwa ndi ankhondo. Ndipo inu mukudziwa zimene zinachitika? Ayuda amenewo anati, "Tsopano ife tibwerere ku nyumba ya Ambuye."

<sup>217</sup> Koma iwo amene anachenjezedwa ndipo atadzazidwa ndi Mzimu Woyera . . .

<sup>218</sup> Monga Josephus anati, "Mtundu wa anthu umenewo wakudya anthu, inu mwakhala mukudya thupi la Yesu uyu wa ku Nazareti." Anati, "Iwo analibisa thupi Lake kutali, ndipo iwo akhala akudya za ilo." Iwo anali kudya mgonero. Ananena kuti iwo, gulu ilo kumbuyo uko, "Osokonezeka awo."

<sup>219</sup> Kodi inu mumadziwa kuti anthu awo kumbuyo uko ankatchedwa "osokonezeka"? Inu mukudziwa zimenezo? Inu mukudziwa chimene *osokonezeka* chiri? Winawake yemwe ali "wopenga." Eya. Taonani pa Paulo Woyera.

<sup>220</sup> Tsopano, inu anthu, inu—inu Abaptisti mumakonda kunena, "Paulo Woyera, o, ine ndikumukhulupirira iye." Inu Akatolika mumati, "O, Paulo Woyera," ndi kumapsyopsyona awiri kapena atatu a mapazi ake kutali, mafano ake kumeneko ku Roma. "Paulo Woyera! Inde, bwana!"

221 Penyani chimene Paulo Woyera ananena pamene iye anali pamaso pa Agripa. Iye anati, “Mu njira imene iwo amayitcha osokonezeka,” woyera-wodzigudubuza, “ndiyo njira yomwe ine ndimapembedzera Mulungu.” Ameni.

222 Ine ndikanakonda ndikanalumikizana naye iye manja; Ine ndikanati, “Ine ndikukhulupirira momwemo, Paulo! Aleluya! Inde, bwana, chinthu chomwecho! Zaka mazana khumi ndi zisanu ndi zinai zadutsa, Paulo. Ine ndikukhulupirirabe chinthu chomwecho!” Ndikadali nawobe Mzimu Woyera; zizindikiro zomwezo, zodabwitsa zomwezo, chirichonse mofanana basi; kumapitirirabe patsogolo, Mzimu Woyera womwewo, kusindikizabe mpaka (liti?) tsiku la chiwombolo.

223 “Uthenga uwu udzalalikidwa...” Chiyani? “Uthenga!” Uthenga ndi chiyani? Osati “Mawu okha.” [M’bale Branham agoda pa guwa kanai—Mkonzi.] Paulo anati, “Uthenga unadza kwa ife, osati mu Mawu okha, koma kupyolera mu Mphamvu ndi kuwonetsera kwa Mzimu Woyera unadza Uthenga.” [M’bale Branham agoda pa guwa katatu.]

224 Paulo anati, “Ine sindinadze ndi maphunziro ena a seminare, kubwera kumapanga mawu amaluwa aakulu, kwa chipulumutso chanu kuti chikakhazikike pa mawu ofufuma ndi milomo yosangalatsa, ndi mayamikiro ena kapena chikhulupiriro cha atumwi, kapena chinachake monga choncho. Ine sindinadze kwa inu monga choncho. Koma ine ndikudza kwa inu ndikudziwa chinthu chimodzi chokha, Mphamvu ya chiwukitsiro cha Yesu Khristu, ndi kuwonetsera kwa Mzimu Woyera.” Aleluya! Mulungu atipatse ife Apaulo ena, ndi nkhonya zazikulu, zamphamvu zimene ziti ziuyale Iwo kunja uko ndi Uthe... wopanda chipika china cha ku seminare chikutsekereza. Ameni. Chisindikizo cha Mulungu! Ameni.

225 Tsopano, kodi ife tiri ndi nthawi yochulukira bwanji? Yambiri, sichoncho ife. [Osonkhana anena, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndicho chimene ine ndinaganiza. Ndizo zabwino. Mawa ndi Loweruka, palibe wa inu amagwira ntchito. Chabwino. Chabwino. Kumbukirani, basi—maminiti pang’ono chabe.

226 Pempherani! Zindikirani, m’bale, iyi ndi nthawi ya kuwona mtima. Iyi ndi nthawi imene ife tiyenera kutenga kulingalira. Ine sindikuyima pano kumasewera chisudzo. Ngati ine ndikanakhala, ine ndikanapita ku guwa ndi kukalapa. Ine mwina ndikhoza kumachita ngati chisudzo kwa ena a inu, koma ine sindikutanthauza kukhala. Ine ndimachita mopusa pang’ono, kamodzi ndi kanthawi; ine sindingakhoze kuzithandiza izo. Chinachake chimafika pa ine, chimandipangitsa ine kuchita monga choncho, kotero ine sindingakhoze kuzithandiza izo. Koma mu mtima mwanga, m’bale, ine ndikukhulupirira Iwo ndi mtima wanga wonse. Kwa zaka makumi awiri zina zosamvetseka ine ndalalikira

Izi kupyolera pa guwa ili, kuzungulira dziko, ndipo Mulungu amatsimikizira Izo ndi zizindikiro ndi zodabwitsa. Amen. “Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse.” Inde.

<sup>227</sup> Tsopano Iye anati, “Apangitseni iwo ali ndi zida kuti abwere patsogolo.” Iwo anakana kulandira chilemba chimenecho. Ndipo Iye anapita patsogolo, ndipo Tito analanda makoma a Yerusalemu, ndipo iwo anathamangira mu mzinda; iwo anawakhalitsa iwo ndi njala mmenemo, mpaka iwo ankaphikirana ana a wina ndi mzake ndi kuwadya iwo. Iwo ankadya khungwa pa mtengo, udzu kutha pa nthaka. Ndiyeno potsiriza pamene iwo amayenera kugonja. . . Tito, pamene iye anapita mu Yerusalemu, iye anawononga kwathunthu chirichonse mkati mmenemo, anapha akazi, ana, makanda, ansembe, china chirichonse, ndi kuwutentha mzindawo.

<sup>228</sup> Ndipo Yesu anati, “Idzafika nthawi imene sipadzakhala mwala umodzi wotsala.”

<sup>229</sup> Anati, “Penyani pa kachisi wathu wamkulu kwambiri. M’bale, ife ndife Abapisti, kapena Amethodisti, kapena Apentekoste, kapena kaya chiyani.”

Iye anati, “Apo sipadzakhala mwala umodzi wotsala pa umzake.”

<sup>230</sup> Zikusonyeza kuti “Mulungu samakhala mu nyumba zopangidwa ndi manja.” Mulungu amakhala mu mitima ya anthu. “Pakuti thupi Inu mwandikonzera Ine.” Mzimu Woyera sumakhala mu nyumba. Iwo umakhala mu mtima. Ndiye kachisi. “Inu simukudziwa ayi kuti ndinu akachisi a Mulungu wamoyo?” Amen. Kumanga kachisi, kumanga tchalitchi chikhulupiriro chanu chonse chamangidwa kuzungulira kachisi wanu kapena mpingo wanu, fano la mtengo, kutenga chilemba cha chirombo ndi kusadziwa izo. Ndiko kulondola. Kumayandama uko ndi kutaya nthawi yanu yonse, alaliki, kuthandizira bungwe lanu, ndi kumapita basi molunjika kumene ku gehena ndi icho monga iwo angakhoze kupitira.

<sup>231</sup> Ine ndikukuuzani inu, m’bale, ndiyo nthawi yoti amuna awuke ndi kulalikira Uthenga ndi Mphamvu ya Mzimu Woyera, pamene paliponse, tiyeni tiwayitane Amethodisti, Abaptisti, Apresbateria, Akatolika, ndi onse, ku mtanda wa Yesu Khristu.

<sup>232</sup> Tsopano, inu mukuti, m’busa wamkulu amanyamula uchi, kuwuyika iwo pa thanthwe. Pamene nkhusa yodwala inkanyambita, iyo inkakhala bwino.

<sup>233</sup> M’bale, ine ndiri nalo thumba lonse la zolemba lodzaza iwo pano, usikuuno. Ndipo ine ndiuyika iwo pa Thanthwe, Khristu Yesu, ndipo nkhusa yodwala ikhoza kunyambita ndi kupeza bwino. Ndiko kulondola. M’bale, mvetserani, osati kuyika izo pa mpingo uliwonse. Izo si za mpingo uliwonse. Izo ndi za pa Khristu. Ndiko kulondola chimodzimodzi.

234 Mawonekedwe! “O, inde, ife timakhulupirira mwa Khristu.” Ntchito zako zimatsimikizira chimene iwe umakhulupirira.

235 Yesu anati, “Zizindikiro izi,” z-i-d-z-a, “zidzawatsata iwo amene akhulupirira, mpaka kumapeto a dziko. Ndipo mu Dzina Langa iwo adzatulutsa ziwanda, kuyankhula ndi malirime atsopano; ngati iwo atatenga njoka, kapena kumwa chinthu chakupha, izo sizidzawapweteka iwo. Ngati iwo ayika manja awo pa odwala, iwo adzachiritsidwa.” Ndicho chimene Yesu ananena. Ndiwo Mawu otsiriza amene anagwa kuchokera pa milomo Yake. Ndipo Iye anatengedwera kupita Kumwamba.

236 Ndipo anthu amene amapita kulikonse, akukhulupirira ndi kulalikirira Machiritso Auzimu, ndi mphamvu za Mulungu, dziko limawatcha iwo “openga.” Ndipo Baibulo linati, “Ngati iwo amamutcha Mbuye wa nyumba ‘Bezebulu,’ mochuluka bwanji iwo ati adzawatche iwo, ophunzira Ake?”

237 Anaweruzidwa, uko iwo ali, onse anafa chimodzimodzi basi. Koma Josephus anati, “Anthu awo amene. . .anthu awo—Akhristu awo a mtundu umenewo, anali atapita kuchokera ku Yerusalemu mpaka ku Yudea, ndi kuthawa mkwiyo wonse uwu.” Tsopano ameneyo anali Myuda, kutha kwa Myuda.

238 Mwamsanga tsopano, kwa maminiti pang’ono otsatirawa, tiyeni titsirize Amitundu, mwamsanga ndithu. Tiyeni titembenuzire ku Chivumbulutso mutu wa 7, kumene ife titi titsirize nyengo ya Amitundu. Tiwone ngati izi ziri zolondola kapena ayi. Apo panali pamene mneneri wa Ezekieli 9 ananenera kutha kwa m’badwo *umenewo*; tsopano apa pali Mzimu Woyera ukunenera kutha kwa m’badwo *uwu*. Mvetserani mwatcheru tsopano pamene ine ndikuwerenga mosamala.

*Ndipo zitatha zinthu izi. . .*

239 Chivumbulutso 7 tsopano, “Zitatha zinthu izi ine ndinawona angelo anayi. . .” Awo anali okwera pakavalo amene anapita, pa mutu wa 6, ndi momwe iwo anapitira; kavalo wotumbululuka, ndi kavalo wakuda, ndi kavalo wofiira, ndi zina zotero, amene, okwera awo anali akuwakwera mdziko kwa nthawi yayitali.

*. . .ine ndinawona angelo anai akuyima pa ngodya zinai za dziko lapansi, akugwira mphepo zinai. . .kuti izo zisawombere pa dziko lapansi, ngakhale pa nyanja, ngakhale pa mtengo uliwonse.*

240 Tsopano penyani masomphenya amene iye anawawona poyamba. “Ine ndinawona angelo anai akuyima pa ngodya zinai,” malo anai kuzungulira dziko lapansi, mngelo, akugwira mphepo zinai. *Angelo* ali “atumiki.” Baibulo linanena choncho. Ndipo *mphepo* ziri “nkhondo ndi makangano.” Iye anali kugwira mphepo zinai, apa, . . .? . . . Tsopano penyani, ndime ya 2.

*Ndipo ine ndinawona mngelo wina akutsika kuchokera kummawa, ali ndi (c-h-i-s-i-n-d-i-k-i-z-o,*



ntchito yotsirizika, mwa kuyankhula kwina) . . . *ali ndi chisindikizo cha Mulungu wamoyo: ndipo iye anafuula ndi liwu lalikulu kwa . . . angelo, . . . amene anapatsidwa kuti awononge dziko lapansi ndi nyanja,*

*Akunena, Musawononge ayi dziko lapansi, ngakhale nyanja, ngakhale . . . mitengo, mpaka ife titasindikiza antchito a Mulungu wathu mu mphumi zawo.*

241 Penyani, ine ndiwerenga mpaka pansi.

*Ndipo ine ndinamva chiwerengero cha iwo . . . amene anasindikizidwa: ndipo apo anasindikizidwa a—a . . . anasindikizidwa zana ndi makumi anai ndi zikwi zinai za . . . fuko la—a . . . fuko la ana a Israeli.*

242 “A fuko la Yuda, khumi ndi awiri . . .” ndipo mpaka pansi, ndi “Benjamini,” ndi “Gadi,” ndi “Rubeni,” mpaka pansi kwa “Zabuloni,” ndipo mpaka pansi kwa mafuko khumi ndi awiri, pa mapeto a ndime ya 8. Ndipo thwelofu kuchulukitsa ka thwelofu ndi chiyani? [Osonkhana anena, “zana limodzi makumi anai ndi zinai.”—Mkonzi.] Zana limodzi makumi anai ndi zinai. “Zikwi zana limodzi makumi anai ndi zinai,” za Ayuda onse. Tsopano, penyani.

*Ndipo zitatha izi ine ndinapenya, ndipo, onani, khamu lalikulu, limene palibe munthu akanakhoza kuliwerenga, la mitundu yonse, malirime, ndi mafuko, . . .*

243 Kodi iwo anachokera kuti? Inu mukuona, ife tikuwona kumene Ayuda awo pa mapeto; ndi pamene angelo anapatsidwa kuti apite patsogolo kuti akawononge, ananena muno, anawona ndipo “atagwira.” Koma kodi awa anachokera kuti, a mitundu yonse, malirime, ndi mafuko. Iwo anawonekera poyera.

*. . . ndipo anthu, ndi malirime, anayima pamaso pa Mwanawankhosa ndi pamaso . . . anavekedwa . . . Mwanawankhosa, anavekedwa ndi miinjira yoyera, ndi kanjeza mu dzanja lawo:*

244 Mkwatibwi, Mkwatibwi wa Amitundu anali atasindikizidwira kutali kuno. Penyani.

*Ndipo iwo analira ndi liwu lalikuru, akunena, Chipulumutso kwa Mulungu wathu amene akukhala pa mpandowachifumu, ndi kwa Mwanawankhosa.*

*Ndi—ndi . . . angelo amene anayima pozinga mpandowachifumu, . . . akulu, . . . zamoyo zinai, . . . anagwa pamaso pa mpandowachifumu pa nkhope zawo, ndipo anapembedza Mulungu,*

*Akunena, . . . (Mvetserani, ngati izi sizikumveka ngati msonkhano wa Mzimu Woyera!) M— . . . Madalitso, ameni, ulemerero, . . . nzeru, . . . matamando, . . .*

*ulemu, . . . mphamvu, . . . ukulu, zikhale kwa Mulungu wathu kwa nthawi za nthawi. Amen.*

245 Izo sizikumveka ngati mtundu wina wa msonkhano wa mwa mwambo wa amadigrii, kwa ine. Izo zikumveka ngati kutsanulira kwa Mzimu Woyera, kwa kachitidwe kachikale, kwa ine. Anthu amenewo anali ali kwinkwake; iwo akudziwa choti achite pamene iwo anawona Mwanawankhosa atakhala pa Mpandowachifumu.

*Ndipo mmodzi wa aakulu . . . anati kwa ine, Awa ndi yani . . . ndipo avekedwa mu miinjiro yoyera? ndipo iwo akuchokera kuti?*

246 Tsopano iwe umawadziwa Ayuda onse, koma nanga awa anachokera kuti, “mitundu yonse, malirime, ndi mafuko?” Penyani.

*Ndipo ine ndinanena kwa iye, Bwana, inu mukudziwa. Yohane anati, “Ine sindikudziwa basi.” Ndipo iye ananena kwa ine, . . .*

247 Awa ndi iwo amene anali ndi Chija, ine ndikuganiza. Chabwino.

*. . . Awa ndi iwo amene anabwera kuchokera mu chisautso chachikulu, (otchedwa “oyera-odzigidubuza,” opangidwa kukhala onyozedwa, ozunzidwa, osekedwa) . . . abwera kuchokera ku chisautso chachikulu, ndipo atsuka miinjiro yawo, ndi kuipanga iyo kukhala yoyera mu magazi a Mwanawankhosa. (Penyani!)*

*. . . iwo ali pamaso pa mpandowachifumu wa Mulungu, . . .*

248 Kodi mkazi amakhala kuti? Kodi mfumukazi imakhala kuti? Ameneyo ndi Mkwatibwi, Mkwatibwi wa Amitundu.

*. . . ndipo iwo akumutumikira iye usana ndi usiku mu kachisi: . . .*

249 Mkazi wanga amanditumikira ine kunyumba, usana ndi usiku. Mwaona? Ameneyo ndi Mkwatibwi wa Yesu; ameneyo ndi Mkwatibwi wa Amitundu.

*. . . ndipo iwo amene akhala pa mpandowachifumu adzakhala pakati pawo.*

*Iwo sadzamvanso njala, . . .*

250 Aleluya! Masiku ogwirira ntchito atha. Chabwino, ife tinkaphonya chakudya chambiri, koma ife sitidzaphonya konse chimodzi Kumeneko. Amen.

251 Ine ndikudziwa mayi anga osauka, aang’ono okalamba akhala pano usikuuno. Ndipo ine ndawawonapo iwo akuchoka pa tebulo. Ife titamwa khofii ndi buledi wina wovunda. Iwo amakhoza kutsanulira uyo apo, kuyikamo shuga wina. Ndipo

popanda wokwanira kuti tigawane; ndipo ana amakhala akulira, ndipo amauka ndi kuyenda kuchokapo. Koma ife sitidzachita konse izo Kumeneko! Bambo anga okalamba anagona pa mikono yanga, mbali ina ya msewuyo, kutsidya uko, ndipo anafa, anjala.

<sup>252</sup> Koma ife sitidzachita konse izo kachiwiri. Aleluya! Ayi, bwana. Kulibenso kumva njala.

*Iwo sadzamva njala ukonso, ngakhalenso kuti iwo adzamva ludzu...ngakhale dzuwa silidzawalira pa iwo,...*

*Pakuti Mwanawankhosa yemwe ali mkati mwa mpandowachifumu adzawadyetsa iwo, ndipo adzawatsogolera iwo mu akasupe amoyo a madzi: ndipo Mulungu adzapukuta...misonzi yonse kuichotsa pa maso awo.*

<sup>253</sup> Iwo mwina akhoza kuti achite kulira pang'ono ndi kumapitiriza, pamene Mzimu Woyera ubwera. Koma Mulungu adzapukuta misonzi yonse kuichotsa mmaso mwawo.

<sup>254</sup> Penyani, iye anawona “angelo anai akuyima pa ngodya zinai, akugwira mphepo zinai.” Mwamsanga tsopano. Nthawi yanga yatha, koma ndiroleni ine nditengere nsonga iyi kwa inu, tisanati titseke. Penyani, iye anawona angelo anai. Iye anawona kutseka kwa mpingo wa Chiyuda, momwe iye anawawonera iwo akubwera njira yomweyo; akubwera ndi zida zache zophera, ankhondo aja.

<sup>255</sup> Tsopano penyani. Kodi ndi chilemba cha mtundu wanji chimene Mpingo wa Mzimu Woyera unalandira, ngati chilemba pa mphumi zawo? Icho chinali chizindikiro chazimu. Mzimu Woyera unawalemba iwo. Ndi kulondola uko? [Osonkhana anena, “Ameni.”—Mkonzi.] Iye sanawadinde kanthu pa mutu wawo. Kodi Iye anatero? [“Ayi.”] Ayi.

<sup>256</sup> Iwo sanatsutsidwe ndi dziko lina lotsutsa-chipembedzo. Iwo anatsutsidwa ndi awo omwe. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Mpingo weniweni wa Mulungu wamoyo udzatsutsidwa ndi Akatolika ndi Aprotostanti, chifukwa iwo adzayanjana palimodzi. Iwo ali kale limodzi ngati amodzi, monga mayi ndi mwana wamkazi.

<sup>257</sup> Koma awa, *apa*, sanali. Ndiye, penyani chimene Iye anachita. Iye anati, “Kayikeni chilemba pa mphumi zawo.” Chinali chilemba cha mtundu wanji icho? Ine ndiwerenga izo kwa inu, Machitidwe 2. “Iwo anali nako onse kumvana kumodzi mu malo amodzi. Ndipo mwadzidzidzi apo panadza mkokomo, Mngelo akubwera kuchokera Kumwamba.”

Inu mukuti, “Kodi Mngelo anali mkokomowo?”

<sup>258</sup> Chinali chiyani icho, chimene chinapita pamaso pa Davide, pamene iye anamva mkokomo wa masamba, masamba a mabulosi, usiku uja pamene iye anali kuwopa kuti apite

kokha patsogolo? “Anamva mkokomo kuchokera Kumwamba ngati mkuntho wa mphepo yamphamvu,” Mulungu akupita patsogolo pawo.

<sup>259</sup> “Ndipo mwadzidzidzi panawonekera kwa iwo Mzimu Woyera ndi Mphamvu.” Panja kupyola mu misewu iwo anapita, akuzandima ndi kulumphu, ndipo akuyankhula mu malirime, ndi milomo yachibwibwi, ndipo akufuula, ndi kumachita ngati chidakhwa, ndipo aliyense akusangalala basi ndi kuyamika Ambuye Mulungu. Kodi nkulondola uko?

<sup>260</sup> Umo ndi momwe Mulungu amachitira pamene Iye atumiza Mphamvu Yake pansi ndi ubatizo wa Mzimu Woyera. Ndipo Iwo unasunthira mkati kumene pamenepo, ndipo panapita Uthenga! Aleluya! Ndipo iwo anafuula ndi kukuwa, ndipo anayankhula mu malirime, ndipo anapita kunja kuja. Ndipo chimenecho chinali chilemba chimene Mulungu anachiyika pa anthu. Nkulondola uko? Mulungu anayika chilemba, ndipo uwo ndiwo mtundu wa chilemba chimene Mulungu ati ayike pa anthu Ake lero. Chisindikizo chomwecho cha Mulungu chimene chinapita pa iwo uko, pansi pa ubatizo wa Mzimu Woyera, chinali chisindikizo cha Mulungu.

<sup>261</sup> Ine ndikufuna ndikufunsemi inu chinachake, mpingo. Baibulo limanena kuti chilemba cha Mulungu, mu tsiku limenelo, chinali ubatizo wa Mzimu Woyera. Chisindikizo chimene chinali pa anthu, kuti chiwapange iwo mosiyana kwa enawo, chinali ubatizo wa Mzimu Woyera. Nkulondola uko? [Osonkhana anena, “Ameni.”—Mkonzi.] Chipangano Chatsopano chinati, mu Aefeso 4:30, kuti Mzimu Woyera ndi chisindikizo cha Mulungu, kwa anthu mu masiku otsiriza, mpaka kopita kwanu Kwamuyaya. Nkulondola uko? [“Ameni.”] Ndiye Mzimu Woyera unali kulondola.

<sup>262</sup> Tsopano, ife tinali nawo m’badwo wa Methodisti, ife tinali nawo m’badwo wa Baptisti, ife tinali nako kulungamitsidwa, ife tinali nako kuyeretsedwa. Ife tinali nazo zinthu zonse izi, zikubwera motsatira.

<sup>263</sup> Ndipo pafupi kumene zaka makumi anai zapitazo, ubatizo wa Mzimu Woyera unaphunziridwa koyamba mu United States. Nkulondola uko? Pafupi zaka makumi anai zapitazo, pamene anthu anayamba kulandira. . .

<sup>264</sup> Tsopano, iwo anakakonda kuyitcha iyo ntchito yeniyeni yachiwiri ya chisomo, kuyeretsedwa. “Kuyeretsedwa,” ndiko kulondola.

<sup>265</sup> Chikho chiyenera poyamba kutengedwa, kunyamulidwa. Icho chonse chadzaza matope. Ndiko kulungamitsidwa, chifukwa m—munthu wachitenga icho.

<sup>266</sup> Chinthu chotsatira, icho chiyenera—kutsukidwa ndi kupukutidwa. Mawu okuti *kuyeretsa* amatanthauza “kutsukidwa, ndi kuyikidwa pambali kuti chitumikire.” Koma

“kuyikidwa pambali *chifukwa* choti utumikire” sizikutanthauza kuti iwe uli *mu* utumiki.

<sup>267</sup> Ndiyeno Yesu anati, “Odala muli inu pamene mumva njala ndi ludzu chifukwa cha chilungamo, pakuti inu mudzadzazidwa.” Onani, Mzimu Woyera unadza pa oyeretsedwa, kwenikweni, owona, okhulupirira oyeretsedwa. Ndipo zizindikiro ndi zodabwitsa zinayamba kuwonekera zokha mwamsanga pamene chikho choyeretsedwacho chinakhala chokonzedwa, ndipo Mzimu Woyera unalowa mkati mwa icho. Mukuona chimene ine ndikutanthauza?

<sup>268</sup> Inu simungakhoze kubweretsa mafuta kuchokera mu botolo kokha ngati muli mafuta mkati mmenemo, ziribe kanthu kaya botololo ndi loyera chotani. Inu simungakhoze kubweretsa kuyankhula malirime, ndi machiritso Auzimu, ndi Mphamvu za Mulungu, kuchokera mu chinachake chimene mulibe kanthu mwa icho. Mzimu Woyera unayenera kubweretsedwa, ndiye.

<sup>269</sup> Penyani, pafupi zaka makumi anai zapitazo...Tiyeni tiganize Chambuyo. Ife tikuwona, pozungulira...Penyani mwatcheru. Uko kunali wolamulira wamkulu amene anapita, Nkhondo ya Dziko lonse Yoyamba; nthawi yoyamba mu mbiriyakale ya dziko lonse, nkhondo ya dziko lonse. Kodi iye anayambira kuti? Molunjika kumene mu Germany. Nchiyani chinachitika? Kusintha; palibe mmodzi amene akudziwa, mpaka tsiku lino, momwe iyo inalekera. Palibe amene akudziwa. Kawerengeni *Kutha Kwa Nkhondo Ya Dziko Lonse*. Mpukutu uliwonse, ine ndawerenga izo. Palibe munthu mmodzi... Chinthu chokha chimene iwo akudziwa, apo panali kulamula kumene kunabwerapo, “Dziperekeni!” Palibe amene akudziwa amene anakupereka iko. Chifukwa chiyani?

<sup>270</sup> O Mulungu! Inu munditcha ine “woyera-wodzigudubuza,” mulimonse, kotero ine kulibwino ndichite mwakumverera kwanga. Penyani! Ndine wothokoza bwanji chifukwa cha Mzimu Woyera kukhala uli pano pa nsanja, kuti uwulule.

<sup>271</sup> Zindikirani. Penyani. Iwo anapita patsogolo, mphepo iliyonse ikubwera mu dziko, zida zamakono, kuti awononge psyiti chirichonse mu nkhondo ya dziko lonse. Koma, zonse mwadzidzidzi, iyo inaleka. Chivumbulutso mutu wa 7, anati, “Ine ndinawona angelo anai akubwera pansu ndi zida zawo zophera. Ndipo apo panapita Mwamuna akubwera kuchokera Kummawa, wokhala ndi chisindikizo cha Mulungu wamoyo; anati, “Gwirani mphepo zinaizo!”

<sup>272</sup> “Zigwireni izo,” chifukwa chiyani? Ayuda sali mu malo oyenera panobe. Ulemerero! Ayuda sali mu malo oyenera panobe, monga Mulungu analonjezera. Iye anawauza iwo kumene iwo ati adzakhale, akuyima kutsidya. Iye anati, “Pamene inu mudzawona mtengo wa mkuyu ukuyika masamba, dziwani kuti nthawi ili pafupi.” Ndipo pamene inu mukuwona

Ayuda akubwerera ku Palestina, dziwani kuti nthawi ili pafupi. M’badwo uno sudzadutsa mpaka zinthu zonse zikhale zitakwaniritsidwa.” Ndipo, abale, mu zaka zisanu ndi ziwiri zotsiriza ndi nthawi yoyamba imene mbendera ya Chiyuda inawulukapo, mu zaka zikwi ziwiri, pamwamba pa Yerusalemu; inde, zaka mazana makumi awiri ndi zisanu. Amen. Ayuda sanali kumene izo zikanati zidzakachitikire, koma Iye anati, “Zigwireni! Zigwireni!”

<sup>273</sup> Chifukwa chiyani, chifukwa chiyani “zigwireni”? Penyani, iwo anali Amitundu ena apabe, pakati pa m’badwo wa Wesile ndi m’badwo wa Pentekoste, amayenera kubwera mkati. Pentekoste asanapite mu M’badwo wa Mpingo wa Laodikaya, apo panali “khomo lotseguka” limene linayikidwa patsogolo pa mpingo; khomo lotseguka, kwa, “Aliyense yemwe ati afune adzamulole iye kubwera ndi kumwa kuchokera ku Kasupe wa madzi a Moyo waulere.” Khomo lotseguka, loyikidwa. O, mai!

Ndipo Iye anati, “Zigwireni izo!” Chifukwa chiyani?

<sup>274</sup> Yesu anati, “Mwamuna anapita kunja ndipo iye anakagwira ntchito. Ndipo mwamuna wina anapita kunja, mu ora lina, ndipo iye anakagwira ntchito. Mwamuna wina anapita kunja ndipo anakagwira ntchito. Ndipo mwamuna mmodzi anapita kunja pa ora la khumi ndi limodzi. Ndipo pamene iye analekeza pa ora la khumi ndi limodzi, iye anawapatsa aliyense wa iwo malipiro omwewo, ora la khumi ndi limodzi. Iwo anadabwa chifukwa chache. Chifukwa chiyani iye, anatenga ora la khumi ndi limodzi, aliyense akubwera mkati?”

<sup>275</sup> Ya Marteni Lutera amene anagwira ntchito, anayenda pansu pa nyengo ya Lutera, anafa mu chisomo!...?....ena, Amethodisti ofuula, amene anafa pansu pa m’badwo wa Wesile, anafa mu chisomo. Ife tikukhala mu m’badwo wina, osati kumbuyo uko. Pano! Amayi adali kumapita mu ngolo, ndipo ife tikuyenda mu Ford ya modelo V-8, pafupifupi yoyendetsedwa ndi jeti. Ndiko kulondola. Ife tikukhala mu m’badwo wosiyana, palimodzi. Ndipo ife tikukhala mu nyengo zosiyana. Ife tikukhala mu tsiku la kubwezeretsa kwa Mphamvu za Mulungu, ndipo pakali pano onani Mphamvu ya Mulungu monga iwo anachitira mu chiyambi. Ife tikukhala mu m’badwo wina. Musati muziyang’ana mmbuyo uko kwa Wesile, Amethodisti, ndi onse awo, Abaptisti, ndi Apresbateria. Yang’anani kuno kwa Yesu Khristu, Woyambitsa ndi Wotsirizitsa wa Chikhulupiriro cha Baibulo. Aleluya!

<sup>276</sup> Tsopano mpenyeni Iye, anati, “Zigwireni izo,” mpaka (chiyani?) anthu a ora la khumi ndi limodzi akhoze kubwera mkati, kuyitana kotsiriza kwa Amitundu. Amayi anagwira ntchito *kumeneko*; adadi ndi iwo anagwira ntchito *kumeneko*; agogo aakazi anagwira ntchito kumbuyo *uko*. Uwu ndi m’badwo wathu, ora la khumi ndi limodzi. Nkhondo ya dziko lonse ija

inaleka mu mwezi wa khumi ndi umodzi mu chaka, tsiku la khumi ndi limodzi la mwezi, ora la khumi ndi limodzi mu tsiku, ndiponso miniti ya khumi ndi imodzi mu ora; kuti anthu a ora la khumi ndi limodzi akhoze kubwera mkati, (chiyani?) kulandira ubatizo womwewo wa Mzimu Woyera umene iwo analandira kumbuyo *kuno* mu chiyambi, kuti akabweretse aponso Mphamvu ndi chiwukitsiro cha Ambuye Yesu Khristu, zizindikiro zomwezo ndi zodabwitsa.

<sup>277</sup> Ndi chiyani icho? Nkhondo zikulimbana *kuno*, kulimbana *uko*; kulimbana *kuno*, kulimbana *uko*; kuyesera ku . . . Mabomba a atomiki ndi china chirichonse ziri kumangidwa, koma iwo sangakhoze kuchita izo. [M'bale Branham agogoda pa guwa nthawi zingapo—Mkonzi.] Iwo sangakhoze kuchita izo mpaka Ayuda atalandira kuchezeretsedwa kwa ubatizo wa Mzimu Woyera. Mngelo anati, “Zigwireni izo, mpaka ife titasindikiza antchito,” osati Mkwatibwi. Amitundu sanali konse antchito; ife ndife ana aamuna ndi ana aakazi. Awo ndiwo antchito, Ayuda. Abrahamu anali wantchito wa Mulungu. Aleluya! Tsopano, tsopano ife tikupeza zikwi kuphatikiza zikwi za Ayuda. Mulungu anawumitsa mtima wa Farao, kuti awathamangitsire iwo ku Palestina. Mulungu anawumitsa mtima wa Hitler, mtima wa Mussolini, mtima wa Stalin. Iye akuwathamangitsa mwa mphamvu, kupita ku Palestina, osadziwa ayi chimene iye akuchita, kugwira ntchito kumene mu manja a Mulungu.

<sup>278</sup> Zikwi zana limodzi makumi anai ndi zinai awo adzayima kumeneko. Ndipo limodzi la masiku awa, wina Waumulungu, woyera, mneneri wodzozedwa wa Mulungu adzapita kumeneko ndi zizindikiro ndi zodabwitsa. Ayuda amenewo adzati, “Ndicho chimene ine ndikuyembekezera.” [M'bale Branham agogoda pa guwa kanayi—Mkonzi.] Inde, bwana. Ndipo Mulungu adzabatiza Ayuda zikwi zana makumi anai ndi zinai.

<sup>279</sup> Ndipo Mkwatulo udzadzaz; m'badwo wa Amitundu udzatha. Bomba la atomiki lidzaphulika ndi kulitenga dziko. Ndipo Mpingo wa Amitundu udzakwatulidwira mmwamba, kukayima kumeneko mu Kukhalapo kwa Mulungu. “Ndi ndani awa amene akubwera kuchokera mu chisautso chachikulu? Amene atsuka miinjiro yawo mu Magazi a Mwanawankhosa. Iwo ali pamaso pa Mulungu, opanda banga.” Amen.

<sup>280</sup> Chilemba cha Chirombo, chitaganya; mipingo, Chikatolika, zonse kumangidwa palimodzi, kupita mu chisokonezeko. Wotsalira, Mkwatibwi wa Mzimu Woyera.

<sup>281</sup> Ndipo anthu lero amene akuseka pa kuyankhula mu malirime, amene akuseka pa machiritso Auzimu, amene akuseka pa uneneri, amene akuseka pa mawonetseredwe a Mzimu; ndipo mzimu womwewo umene unawalamulira Ayuda awo kumbuyo kuno, amene anachitira mwano Mzimu Woyera kumbuyo uko, ndipo anafa pansu pa chiweruzo Chaumulungu. United States

uyu walunjika ku chiweruzo Chaumulungu, pansi pa Mphamvu ya Mzimu Woyera. Iwo atsutsa, ndi kuseleula, ndi kukana, ndipo kutitcha ife “oyera-odzigudubuza” ndi china chirichonse. Koma ora liri pano, pamene Mulungu ati adzatsanulire chiweruzo Chake Chaumulungu. Amen.

<sup>282</sup> Khalani okonzeka. [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] . . .? . . . Malo okhawo otetezeka amene alipo lero ndi mwa Khristu Yesu. Mulungu akudalitseni inu. Ngati inu simuli mkati, kanikizani mpaka inu mutalowa mkati. “Iwo amene ali mwa Khristu Yesu ndiwo Mulungu adzawabweretse limodzi ndi Iye mu kudza Kwachiwiri.”

<sup>283</sup> Wopanda chisindikizo cha Mulungu, chimene chiri ubatizo wa Mzimu Woyera, chitaganya cha chinyengo ndicho chilemba cha chirombo. Ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Koma aphunzitsi a chipembedzo awa akuyesera kuchiyika icho pa chikominisi, pamene iwo sakuzindikira kuti icho chikugwira ntchito pakati pawo pomwe. Iye anati, “Adzakhala atsogoleri akhungu a akhungu.” Iye anati, “Adzakhala nawo maso, koma osakhoza kupenya.” Anati, “Inu, ndipo mu miyambo yanu, mumayankhula chiphunzitso cha anthu, mumapanga malamulo a anthu, kupanga malamulo a Mulungu opanda mphamvu.”

<sup>284</sup> Inu muwaseka Akatolika chifukwa chokhazikitsa katekizimu yawo, ndipo anthu anu amapita kuno ku msonkhano wina kapena chinachake, ndi kuganizira ngati iwo angakhoze kulandira machiritso Auzimu, kapena ubatizo wa Mzimu, ndi zinthu izi. Ndipo iwo amawutsutsa Iwo ndi kuwukanira Iwo pansi. Ndipo inu mumaseka pa Katolika. Inu mulibe ufulu kuti muziseka pa Katolika. Chifukwa, ngati iye anali “HULE,” Baibulo linati ndinu “KAHULE,” mu chitaganya chomwecho.

<sup>285</sup> “Tulukani kunja pakati pa izo, anthu Anga! Khalani inu olekanitsidwa,” atero Mulungu, “ndipo Ine ndidzakulandirani inu kwa Inemwini.” Ndiko kulondola.

<sup>286</sup> O, chifukwa chiyani Branham Tabernacle osabwera kunja kwa kwinya lathu? Ine ndikufuna kudziwa ngati anthu inu kuzungulira pano mumakhulupirira Uthenga uwu. Ndipo Inu walalikidwa, ndipo inu mwawuwona Iwo, zizindikiro ndi zodabwitsa, ndi kutsimikizidwira. Ndi chirichonse chimene Ambuye wayankhula, chafika pochitika. Ndiye, chavuta ndi chiyani kuzungulira pano, pamene ine ndikumva kuti pali makangano pakati panu, pamene ine ndikumva kuti pali ndewu? Ine ndikufuna inu mulembe chimene chiri vuto ndi inu, chimene chiri pa mtima wanu, ndi kuchiyika icho pa guwa la pa nsanja, mawa usiku. [M'bale Branham anagogoda pa guwa nthawi zingapo—Mkonzi.]

<sup>287</sup> Ine ndikufuna kuwona chifukwa chimene mpingo uwu sungakhoze kunyamulidwira kutali ndi Mphamvu ya Mulungu,



ndi ubatizo wa Mzimu Woyera, ndi zizindikiro ndi zodabwitsa. Chavuta ndi chiyani? Abusa anu amakhulipirira Izo. Inu mumakhulupirira Izo. Kotero, chavuta ndi chiyani pano? Pali chinachake chalakwa. Iyi inayenera kukhala nyumba yowunikira kwa dziko. Awa anayenera kukhala malo amene Mphamvu za Mulungu, ndi kulira ndi kufuula, ndi kufunafuna Mulungu, ziyenera kumapitirira, usana ndi usiku. Nchifukwa chiyani ife sitingakhoze kukhala nazo izo?

<sup>288</sup> “Ine ndikufuna, koma inu simukufuna,” anatero Yesu. “Inu simukufuna. Bwerani ndipo dzaguleni kwa Ine.”

<sup>289</sup> “Ine ndikudziwa inu mukuti,” Iye anati, “inu ndinu ‘olemera, anali osasowa kanthu,” akuyankhula kwa mipingo. Anati, “Inu mukuti, ‘Ine ndine wachuma, ndipo ine sindisowa kanthu. Ndife bungwe lalikulu.’ Ndipo inu simukudziwa, koma ndinu atsoka, osauka, omvetsachisoni, akhungu, ndi amaliseche, ndipo simukudziwa izo.” Ngati munthu ali mu vuto limenelo ndipo nkudziwa izo, iye adzithandiza yekha. Koma, pamene iwe uli mnjira imeneyo, “ndipo osadziwa izo!” Ndipo Khristu ananena kuti mipingo mu tsiku lino idzakhala mwanjira imeneyo, ndipo iyo siyikanadziwa izo.

<sup>290</sup> Tsinani umunthu wanu wauzimu, wokondedwa wanga, m’bale wokondedwa. Tsinani moyo wanu, monga izo zinali, ndi pemphero, ndi kunena, “Ambuye Yesu, fufuzani pa ine. Ndiroleni ine nditenge kusinkhasinkha usikuuno, ine ndisanapite ku kama, ndi kupeza chomwe chiri vuto ndi ine. Ine ndakhala ndikudzinenera kwa zaka, ndipo ine sindikuwona zinthu izi zimene Yesu ananena. Kutu Iye adzakhala ndi ine, ndipo zinthu izi zidzapitirirabe, ine sindikuziwona izo. Chavuta ndi chiyani, Ambuye Yesu?”

<sup>291</sup> Khalani owona mtima. Khalani odzipereka. Bwerani pansu ndi kuyankhula naye Iye, ngati maso ndi maso ndi m’bale. Iye akuululirani inu. Iye akuuzani inu. Ng’ambani moyo wanu pakati, ndi kuwugoneka iwo kunja uko. Nenani, “Ambuye Yesu, ngati chinditengera ine banja langa, ngati chinditengera ine moyo wanga, ngati chinditengera ntchito yanga, ngati chinditengera umembala wanga, ngati icho chinditengera kutchuka kwanga mu mzinda, ine nditenga njira ya onyozedwa ochepa a Ambuye.”

<sup>292</sup> Tsopano kumbukirani, Yesu anati, “Khwalala ndi chipata, ndipo njirayo ndi yopapatiza, ndipo koma padzakhala ochepa amene ati adzayipeze iyo. Pakuti yotakata ndi njira yopita ku ziwonongeko.” Milioni ena mu ‘54, “Chotakata ndi chipata chopita ku chiwonongeko, ndipo ambiri kumeneko adzakhala amene ati adzapite mu imeneyo.” Ndiko kulondola. “Iye amene ati adzataye moyo wake chifukwa cha Ine adzawupeza iwo. Iye amene akonda abambo ake, amake, mlongo wake, m’bale wake, kapena chirichonse, moposa Ine, sali woyenera kutchedwa

Wanga. Iye adzayika dzanja lake pa khasu ndi kuwuyamba wapatsogolo, ngakhale kupotoloka kuti ayang'ane kumbuyo, sali woyera nthawiyo." M'bale!

<sup>293</sup> Limodzi la masiku amenewa, ulaliki wotsiriza wa Uthenga wodzozedwa ndi Mzimu Woyera udzalalikidwa. Limodzi la masiku amenewa, mfuti yotsiriza idzawombidwa. Limodzi la masiku amenewa, nyimbo yotsiriza idzayimbidwa. Limodzi la masiku awa, pemphero lotsiriza lidzapempheredwa. Limodzi la masiku amenewa, zitseko za kachisi zidzatsekedwa kwa nthawi yotsiriza, Baibulo lidzatsekedwa pa guwa. Ndipo inu mudzayima mu Kukhalapo kwa Mulungu, kuti mukapereke kulongosola pa chimene inu mwamva usikuuno. Nchiyani ndiye? Nchiyani ndiye? Pamene Bukhu lalikulu liti lidzatsegulidwe, nchiyani ndiye? Pamene usikuuno udzabwere pa kawundula, nchiyani ndiye? O, monga nyimbo imanenenera:

Nchiyani ndiye?

Pamene Bukhu lalikulu liti lidzatsegulidwe,  
nchiyani ndiye?

Pamene iwo amene anakana Mpulumutsi lero,  
Adzakhala atafunsidwa kuti apereke  
chifukwa, nchiyani ndiye?

<sup>294</sup> Ntchito yako inayima pa njira yako. Makolo ako anayima mu njira yako. Mzako wamwamuna anayima mu njira yako. Mzako wamkazi anayima mu njira yako. Mpingo wako unayima mu njira.

Nchiyani ndiye? Nchiyani ndiye?

Pamene Bukhu lalikulu lidzatsegulidwa,  
nchiyani ndiye?

Pamene iwo amene akukana Uthenga uwu  
usikuuno,

Inu muti...mudzafunsidwe kuti mupereke  
chifukwa, nchiyani ndiye?

<sup>295</sup> Inu mukachita chiyani nacho icho? Inu mukudziwa chimene chilemba cha chirombo chiri. Inu mukudziwa chimene chisindikizo cha Mulungu chiri. Izo ziri kwa inu.

Alole Ambuye kukudalitsani inu, pamene ife tikuyima.

<sup>296</sup> Inu, Atate Akumwamba, mulole zifundo Zanu ndi madalitso zikhale pa anthu. Mulole Mzimu Wanu usunthe. Ndipo mulole Mzimu Woyera Wanu ukankhire pansu pa anthu, ndi kupereka kwa iwo, Ambuye, ubatizo wa Mzimu. Mulole mwamuna aliyense ndi mkazi, mnyamata ndi msungwana, muno, mulole iwo atengedwere kutali chotero usikuuno, mwa Mzimu Woyera, kuti iwo adzati, "Mulungu, tengani zonse zimene ine ndiri nazo. Tengani chirichonse chimene ine ndiri. Koma, mundirole ine ndikutumikireni Inu, Ambuye wanga. Ine ndiyika pambali chirichonse. Ine ndidzipereka ndekha. Ine ndikusiya kunyada kwanga. Ine ndikusiya mpingo. Ine ndikusiya chirichonse."

297 Osati kuti iwo akachite kuchoka mu mpingo wawo, Ambuye, koma iwo ayenera kubwera kuchokera mu chikhalidwe chimene iwo ali kukhalamo. O Mulungu, atumizeni Achimethodisti kubwerera ku mpingo wawo, akuyaka, kuti akalalikire Uthenga; atumizeni Achibaptisti abwerere, atumizeni Achikampubelo abwerere, atumizeni Akatolika abwerere. Ambuye Mulungu, tumizani winawake kuchokera mu Branham Tabernacle muno, abwerere ku kachisi pano, ali ndi mzimu wofatsa, wodzichepetsa, amene ati apite konse ndi kukayankhula, ndi kukonda, ndi kuyesa kuwatengera anthu mwa mtima umodzi kachiwiri, kotero Mzimu Woyera ukhoza kubwera mkati ndi kuwagwiritsa ntchito anthuwo. Tumizani zizindikiro zazikulu ndi zodabwitsa. Dzozani wokhulupirira aliyense. Khululukirani tchimo lililonse.

298 O Mulungu, ife tikuwona zizindikiro zikuwonekera. Ife tikuwona mtengo wa mkuyu ukuyika masamba ake. Ife tikudziwa kuti nthawi yayandikira. Ife tikuwona bomba ilo limene liri kutsidya mu manja mwa munthu kumene amene inu munati anapatsidwa kuti adzawononge dziko.

299 O Mulungu, ife tingakhoze bwanji kukana motalikiranso? Tingakhoze bwanji ife? Pamene, ife tikumva Uthenga Wanu wodala ukuyimba momveka kwambiri, momveka; kumva Mzimu Woyera ukutogolera; kuwuwona Mzimu Woyera ukupereka zizindikiro ndi zodabwitsa; kuchiritsa odwala, kutsegula maso akhungu, kubwezeretsa moyo kwa akufa; zodabwitsa zazikulu ndi zizindikiro; Uthenga wayamba kulalikidwa ndi anthu osaphunzira, mbuli, kulalikidwa pansu pa Mphamvu ndi kuwonetsera kwa Mzimu Woyera; zizindikiro ndi zodabwitsa zikuwutsata mpingo. Mochulukanso bwanji!

300 Inu munati, “Ngati inu mukanamudziwa Mose, inu mukanalidziwa tsiku Langa.” Aleluya! Kotero izo ziri lero, Ambuye. [M’bale Branham agogoda pa guwa katatu.] Iwo akuwona zizindikiro za mitundu yonse, za nkondo ndi mavuto, ndi chirichonse. Aloleni iwo atembenezire mmbuyo masamba a Baibulo lakale lokonedwa, ndi kuwona pamene chikhomo cha mtunda chiri. Ife tiri pa mapeto a m’badwo.

301 O Mulungu, sunthirani Mzimu Wanu pa anthu awa. Ndipo pamene iwo azichoka pano, usikuuno, mulole Mzimu Woyera usunthe ndi iwo.

302 Ndipo mawa usiku, Ambuye, pamene ife tibwera pansu ku kuyitanira pa guwa kwakukulu uku kumene ife tikukonzekera kukupereka, ife tikupemphera kuti maguwa akathamangiridwe modzaza, zipinda za pemphero zikadzaze.

303 Ndi mulole, Lamlungu mmawa, Ambuye, ndi Lamlungu usiku, ife tikhale tikuwabatiza anthu pano molingana ndi Mawu a Mulungu. Ndipo mulole Mzimu Woyera ukhale ukugwa

pa madzi amenewo, ndi kumachita zizindikiro zazikulu ndi zodabwitsa. Perekani izo, Atate.

<sup>304</sup> Dalitsani m'busa wathu wokonededwa pano. Dalitsani mamembala. Dalitsani alendo mu zipata zathu. Mulole ife tipite kwathu usikuuno ndi kukalingalira zinthu izi mu mtima wathu; kukabwereranso mawa usiku, tikusangalala, tikubweretsa limodzi nafe mitolo. Ife tikupempha mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni.

<sup>305</sup> Ambuye Yesu Khristu adalitse aliyense wa inu. Gwiranani chanza wina ndi mzake. Mukabwererenso mawa usiku, mukubweretsa chopempha chanu ndi chimene inu mukufuna, ndi kuchiyika icho pa guwa. Mulungu azikudzozeni inu nthawizonse, akhale ndi inu! Ameni. Mulungu akudalitseni. 🐦

*CHISINDIKIZO CHA MULUNGU* CHA54-0514  
(The Seal Of God)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham wolalikidwa mu Chingelezi pa Lachisanu usiku, Mei 14, 1954, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Kumasulira uku kwa Chichewa kunadindidwa mchaka cha 1996 ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©1996 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)